


MPHAMVU YAPAMWAMBA

 Ine ndikuchitabe phwando, nawonso, pa dalitso lija mmawawu. O, mopitirira, mochuluka, ndi zosadziwika, zinthu zimene Mulungu angachitichitire ife pamene ife tidzisonkhanitsa tokha pamodzi! Kodi inu mwazindikirapo chipangireni ife kudzipereka uku kwa Mulungu, momwe zinthu zakhala zikuchitikira muno? Dalitso pambuyo pa dalitso, mphamvu pambuyo pa mphamvu, ulemerero pambuyo pa ulemerero! Zangokhala zodabwitsa. Ndipo Iye apitirira kuchita chotero. Timipango iti, ine ndatipempherera ito, kuti—kuti ena pano amene tiri tawo.

² Tsopano ine ndikungofuna kuthirira ndemanga apo, mphindi chabe kapena ziwiri, ndipo poyamba kukuthokozani nonsenu chifukwa cha mphatso yanu yopambana ya Khristimasi, ya suti ya zovala zomwe mwandibweretsera ine. Kodi izo ndi zomwe zinali mwanunso, M'bale Neville? [M'bale Neville ati, “Inde, bwana. Inde, bwana.”—Mkonzi]. Inde, bwana. Eya, suti ya zovala. Bwanji, alaliki nthawizonse akhoza kugwiritsa ntchito suti ya zovala. [“Zikungondikwanira ine mwangwiro.”] Zodabwitsa, izo nzabwino. Tsopano, iwo amachita thukuta, ndipo thukuta limenelo limavunditsa zovala msanga kuposa chirichonse chomwe ine ndikuchidziwa, mukuona, ndipo zimangotengera zovala zambiri kuti zimusunge mlaliki. Ndi zovala zabwino... Chovala cha thonje lotchipa kwenikweni likhoza kungovunda, mwakanthawi kochepa. Kotero—suti yabwino monga imeneyo itenga nthawi kuti ithe.

³ Ndipo tangoganiza, inu mukuthandizira ndi kupereka zovala izi kwa antchito a Ambuye. Ndipo Ambuye akudalitseni inu. Yesu anati, “Mu zonse zomwe munachitira kwa ang’ono a abale Anga awa, inu mwachitira izo kwa Ine.” Kotero choncho inu simunabweretse, kugulira atumiki awiri suti; inu mwagulira Yesu masuti awiri. Ha-a. Izo ndi zomwe Iye ananena, “Inu mwachitira izo kwa Ine.”

⁴ Koma kukhudza kwakung’ono kwa Kumwamba kuja, mmawa uno, kodi inu munakuzindikira iko? Popanda kuyitanira kuguwa, popanda chirichonse; koma kungoti Uthenga utatha ndipo—ndi chitsitsimutso cha Mzimu Woyera chikusambitsira pa anthu, ulemerero wa Mulungu ukuyenda, iwo anangoyamba kubwera mmwamba, ndi mmusi,ponse pozungulira. Ndipo ine ndinazindikira amzanga ena abwino kwenikweni Achibaptisti, ochokera ku Mpingo wa Baptisti wa ku Walnut Street, mu Louisville, atayima mu kampata, akungosamba mu mphamvu ya Mulungu. O, mai! Ndipo ine ndinakomana nawo iwo utatha msonkhano, iwo anati, “Ndiyo mphamvu ya Mulungu.”

Ine ndinati, “Uko nkulondola. Mwalondola zedi, inu mwalondola ndithu.”

⁵ Mphamvu ya Mulungu! Ndipo iwe siwungapeze mawu akuti unene. Iwe siwudziwa choti unene. Mzimu Woyera umangotenga msonkhano ndipo iwe siwudziwa chomwe Iye ati achite nawo Iwo. Mwakachetechete, mokoma, modzichepetsa, mosweka. O, M’bale Pat, uko ndi Kumwamba basi, kwa ine. Ine ndangokhala mmodzi wa awa a mtundu wachikale amene amakonda kumverera koteroko mkati Mwake, mukuona.

⁶ Monga malemu Paul Rader, iye anati kwa ake...Nthawi ina iye amanena nthano. Ndipo iye anati iyeyo ndi mkazi wake anali atakhala pa tebulo, ndipo iye anafuna kupita kwinakwake kapena kukachita chinachake, ndipo iye amangonena kwa iye, “Ine sindingachite ichi basi,” ndi zina zotero, ndipo iye amakhoza kumuduliza iyo msanga pang’ono.

⁷ Kotero iye anachewukira pozungulira pa iye, ndipo misonzi inali kutsikira mmasaya ake, ndipo iye anati kwa iye, iye anati, “Chabwino, tsopano,” naganiza mu mtima wake, “ngati iye ali wophweka chotero kupwetekedwa, ingomusiyani iye akhale wopwetekedwa.” Kotero iye, monga mwachimuna, iye anapindira pepala lake nalgoneka ilo pansi pa mbale yake.

⁸ Ndipo mkaziyo nthawizonse ankayima pakhomo namupsyopsyona posadzikana; ndiyeno iye akatuluka pa chipata, iye amakhoza kugwedezera dzanja pa iye, ndiyeno izo zimakhoza—izo zimakhoza kusamalira icho, inu mukudziwa, mpaka iye atabwerera kuchoka ku ntchito yake.

⁹ Ndipo kotero m’mawa umenewo, anati, pamene iwo anayamba kutuluka, bwanji, a . . . pakhomo, bwanji, iye anayima pakhomo, ndipo iye anamupsyopsyona natulukira ku mapeto a chipata, natsegula chipata nayang’ana m’mbuyo, ndipo iye anali atayima pakhomo ataweramitsa mutu wake pansi, atapwetekedwabe, akuti iye anagwedeza ndapita, nati iye anagwedeza pitani.

¹⁰ Nati iye anawuyamba kutsikira mu msewu, ndipo iye anayamba kuganiza, “Bwanji ngati china chitachitika kwa ine ndisanabwerere kunyumba, kapena, bwanji ngati china chitamuchitikira iye ine ndisanabwerere mmbuyo, Mulungu akhoza kutichotsa ife pano; ndipo monga mkazi wabwino monga iye wakhala aliri, ndi momwe iye aliri wokoma, ndi zina zotero?” Ndipo anati, iye popitirira kutali, ndi pamene mtima wake umayamba kutupa kwambiri.

¹¹ Kotero iye anangopotoloka nathamangira mmbuyo, anatsegula chipata, nathamangira m’nyumba, natsegula chitseko. Ndipo pamene iye anatsegula chitseko, iye anamva chinachake chikulira. Anayang’ana pozungulira, iye anali atayima kuseri kwa chitseko. Nati iye sanati, “ndikhululukireni ine,” iye sanati “ine ndikupepa,” iye sananene kanthu. Akuti

anangomugwira mkaziyo namupsyopsyonanso iye, napotoloka kuzungulira natulukiranso mmbuyo. Akuti iye anatulukira pa chipata, nati mkaziyo anali atayimanso pakhomopo. Iye anati, “Ndapita.” Ndipo iye anati, “Pitani,” nati, monga iye anachitira nthawi yoyamba, koma nthawi yotsiriza anali ndi kukhudzidwa mkati mwake.

¹² Kotero umo ndi momwe ziriri. Pamene muli ndi kukhudzidwa mkati mwake, mukuona, kuti ndi chinachake chenicheni chochokera kwa Mulungu.

¹³ Tsopano mu kusankha mphindi zochepa zapitazo, kwa trastii watsopano, M'bale Sothamann. Ine ndikutsimikiza kuti matrastii, ndi onse, akudziwa tsopano, kuti, pakutha pa chaka cha chuma, loyamba la Januwale, kuti mauding onse a mpingo, monga abusa ndi madikoni, ndi ena otero, amatha. Ndiye ngati iwo akufuna kupitiriza. . . Osati abusa; ine sindimatanthawuza izo. Ine ndimatanthawuza matrastii, ndi madikoni, ndi aphunzitsi a Sande sukulu, ndi ena otero. Kutu, m'busa amasankhidwiramo ndi mpingo, ndipo iye amakhalabe mpaka, mpaka. Ndiyeno—ndiye iwo. . . Ngati anthu, gulu limene liripo la matrastii, kapena madikoni, kapena aphunzitsi a Sande sukulu, kapena ndani owonjezerapo, ngati iwo akufuna kupitirirabe, iwo amangopitirirabe. Ngati iwo satero, ndiye iwo ayenera—iwo ayenera kusiya ngati iwo sakufuna kupitirirabe; ndipo palibe chinthu chowatsutsa iwo. Ndiye iwo amapitirirabe kwa chaka chotsatiracho. Ndipo—ndiyeno ngati iwo sapitirirabe, ndiye iwo akhala ndi chisankho, ndi kukhazikitsa trastii wina, kapena—kapena udindo uliwonse umene unali.

¹⁴ Chotero, sizimamukanikiza munthu pansu, kwa nthawi ya moyo wake, kuti akatumikire mu gululo. Koma pokha ngati iye akuwona kuti Mulungu ali naye ndipo akumuthandiza iye, ndipo iye akufuna kuchita gawo lake, kapena gawo lake, chirichonse chimene chingakhalepo, kuti apitirirebe ndi ntchito ya Mulungu, ife nthawizonse timakhala okondwa kuwawona iwo akutumikira limodzi naye. Mwaona? Koma njira iyo imamupatsa munthu mwayi woti akatumikire kwa chaka nawona momwe iwo akuyikondera iyo. Ena mwa matrastii athu amapitirirabe kwa zaka ndi zaka ndi zaka, ndi madikoni nawonso, ndipo izo ndi zabwino mwangwiro. Komano palibe nthawi yokhazikitsidwa. Ngati trastii, kapena m'busa, kapena winawake pa gulu, sakuwona ngati iwo angatumikirensa mopitirira, kapena akuchokapo, ndiye iwo angowudziwitsa mpingo, kuti iwo akhoza kupeza wina mmalo awo.

¹⁵ Ndipo izo ndi zomwe zachitika kuno usiku uno, ndi M'bale Morgan, M'bale William Morgan akusiya ngati trastii. Iwo anafuna trastii wina. Ndipo M'bale Sothmann anatchulidwa ngati trastii, mu nthawi yina, ndiyeno usiku uno analandiridwa pa gulu.

¹⁶ Ndi zovomerezeka, malingana monga mpingo. Mu mpingo wathu, ndi kuyima pawokha kwa mpingo. Mpingo umachotsa, kapena kulowetsa trastii, mpingo umachotsa m'busa, kapena kuyikamo m'busa, chirichonse chimene chiri, ndi mpingo mwa zonse. Ndimu mwautumwi. Umo ndi momwe zinkachitikira mu nthawi ya Baibulo. Koteru, ife tikuwona kuti si munthu mmodzi, ndiye, ndi wolamulira mwaukali kapena chinachake mu mpingo. Ife sitikufuna zimenezo. Munthu aliyense, munthu aliyense, inemwini, poponya voti kwa aliyense, ndiri ndi voti imodzi yokha, chimodzimodzi ndi munthu wina aliyense wa mpingo kuno, voti imodzi yokha. Ziribe kanthu zomwe ine ndinganene; ndi zomwe mpingo unganene, onani, zomwe mpingo ukunena mu thupi. Inu mukuzikonda izo? [Osonkhana ati, "Amen."—Mkonzi]. O, ine ndikuganiza kuti izo ndi Mwamalemba basi. Umo ndi momwe ziyenera kukhalira.

¹⁷ Tsopano, ili likhala sabata lopambana kwa ine, tikafika, mawa, Ambuye akalola. Ine ndiyenera kulingalira za chaka chomwe chikudzachi, za kuyitanidwa konse. Ine ndikufuna kupita kunja—ku ofesi ndi kukatenga zondiyitanira zonse ndi kuzibweretsa izo kunyumba. Ndipo chotero, kwa masiku pang'ono otsatirawo, ine ndipita kukapemphera, kwa Mulungu, ndi kupemphera kwa Iye kuti anditsogolere ine nandisonyeza ine njira yoti ndipiteko ndi choti ndichite. Ife sitikukhala mu nthawi monga zinali pamene Iye anali kuno, pamene Mulungu ankamutsogolera Iye kuchokera pa malo kupita kumalo, ndipo Iye amakhala mu mzinda kwa maora pang'ono napita ku mulaga wina. Koma lero ziri mwa kachitidwe kosiyana, ndi dongosolo, magulu a atumiki ndi zinthu zambiri zomwe ziyenera kuchitidwa.

¹⁸ Ndipo momwe ine ndimachitira izo, ine ndimasonkhanitsa zondiyitana zonse za ku Afrika ndi kuziyala izo pansu, zonse zondiyitana za ku India, ndi zonse za ku California, ku Utah, ndi zondiyitana zosiyana zonse, ndipo ndimazisiya izo padera mu miyulu. Ine ndimangoziunjika. Ndiyeno ndimapita kokayenda ndi kupemphera, mwina kulowa mu galimoto langa ndi kuchokapo kwa tsiku kapena awiri. Kubwerera, kupemphera. Chinachake chimadza pa mtima wanga kuti ndipite ku malo ena ake, ndiye ine ndimawona ngati chiri chongondikhudza. Ndiye, kenako, ndiye ine . . . ngati chikundikhudza ine molimba, ine ndimapita kwa mulu uwu komwe malo akutiwa ali, ndiye ndimatenga kalata ndi kuyiwerenga iyo, ya kundiyitana, kuti ndiwone kuti ndi ya kuti. Ndiye, kuyambira pamenepo.

¹⁹ Chifukwa chimene ndimachitira izo ndi ichi. Inu muganize za kuwuluka pafupi maora makumi asanu ndi awiri mphambu awiri pa ndege, mu mikuntho, ndi kukwera ndi kutsika, ndi kutembenezidwa, ngati inu munakwerapo popita ku tsidya la nyanja. Simudziwa nthawi zina kuti muli—muli mmwamba, ndipo nthawizina ili mmusi, ndi kumaponyedwa, pendapenda,

ndi kuzyolima, kupyola mu mitambo imeneyo ndi kuwoloka pa madzi, kwa masiku atatu ndi usiku. Ndiyeno iwe umakatsika pa nthaka, ndipo chinthu choyamba kukumana nawe ndi Satana, “Chabwino, gulu la atumiki linati *izi*, ena mwa iwo atagawanika pa voti, ndi ena olola.” Mwaona?

²⁰ Ndiye inu mukhoza kunena kuti, “Chabwino, mwina Ambuye sanafune kuti ine ndibwere.”

²¹ Koma pamene inu mwatumidwa ndi Mulungu, inu muli okonzeka kukumana ndi m’dani. Inu mukuti, “Ine ndikutsika kuno, mu Dzina la Yesu Khristu. Ine ndadza mu Dzina la Ambuye Yesu, ndipo ndikhala kuno mpakana ntchito Yake itakwaniritsidwa.” Onani, ndiye ndinu okonzeka kukumana ndi zimphamvu.

²² Kotero, inu mumandikonda ine, ine ndikudziwa inu mumatero. Kotero ndipempherereni ine sabata ili, kuti ine ndilingalire moyenera, mwa kudzoza kwa Mulungu kunditsogolere ine.

²³ Tsopano ine ndikakhala ndi ochepa pang’ono, zomwe ine ndimatcha, misonkhano yaing’ono yongodumphira. Ine ndikupita kumusi mu Florida, 8, 9 ndi 10 wa mwezi uno; kapena, Tifton, Georgia. Tifton, Georgia, 8, 9 ndi 10 ya Januwale, ine ndimati nditi, mmalo mwa mwezi uno. Ndiyeno ine ndiyenera kupita ku Glasgow, Kentucky; ndipo mwina Somerset, Kentucky; ndipo usiku umodzi, ndipo mwinamwake Campbellsville, Kentucky. Ndipo—ndipo M’bale Rogers amafuna ine ndibwere kwa usiku umodzi, ku malo awo, kumene ife tiri ndi . . . tinamuphonya iye nthawi ina.

²⁴ Tsopano, mupempherereni M’bale Rogers. Ife tinali ndi chiyanjano, lero, ndipo ine ndinagwira dzanja lake ndipo ndinamupeza iye asali mwaubwino, mwathupi. Kotero mumupempherere M’bale Rogers ali apayu. Iye wadzitengera zinthu zambiri mmanja mwake kumeneko, ndipo zamuchititsa iye chinjenje ndi kuyipidwa, ndipo iye—iye ali mu umoyo woyipa ndithu pakali pano, ndipo mkazi wake ali moyipa kwambiri. Kotero pemphererani anthu awiri ang’onowo, ana abwino zedi a Mulungu. Ndipo ine ndinamuwuzwa iye kuti, Ambuye akalola, ndidzamupeza iye usiku.

²⁵ Ndipo M’bale Ruddell, wamng’ono wathu . . . umodzi wa mipingo yathu, kuno apa pa 62, mnyamata wokulirapo pang’ono wamanyazi, anadutsa kuno ndipo osayang’ana konse mmwamba. Ndipo iye amakhoza kubwera kunyumba. Ndipo, o, ine ndikuganiza kuti anthu amaganiza kuti iye ndi wosautsa nthawizonse, koma panali chinachake cha mnyamatayo chimene chimawoneka chenicheni. Ine ndimangokhala nayebe iye, ndi kukhala nayebe, kuti, “M’bale Ruddell, iwe ukhoza.”

26 Iye anati, “M’bale Branham, ine ndikafika pa chigulu, wanga—mtima wanga umafika pakhosi panga, ndipo ine—ine—ine sindingathe konse kunena liwu.”

27 Ine ndinati, “Uzingoyima pamenepo niwuumezera iwo mmbuyo, ndi kulankhula mu Dzina la Ambuye, waona.” Ndipo tsopano iye ali ndi Kachisi wofanana ndi uyu, kuno pa msewu waukuluwu, kumangochita chinachake. Pitirira nacho. Mnyamatayu anali ndi kuyitana kwa Mulungu. Ine ndikuwadziwa bambo ake ndi mayi ake, iwo ndi anthu abwino zedi.

28 Ndiyeno tikuyenera kudzakhala ndi Junie, usiku umodzi, komwe mu New Albany. Ndipo, o, inu mukudziwa, timisonkhano tating’ono chabe, tomwe nditi ndidzatenge usiku kuno ndi usiku uko.

29 Mpakana, ngati chirichonse chikonzeka molingana ndi dongosolo, cha pa 25 ya Januwale, ine ndidzakhala ndikuchoka kupita ku Miami, ku Msonkhano Waukulu wa Dziko lonse wa Anthu a Malonda a Full Gospel. Ndipo kuchokera kumeneko, ku Kingston, Haiti, kumusi chaku South Amerika, ndipo mpaka kupyola Mexico. Ndipo kuchokera kumeneko, kupita ku Afrika. Kuchokera ku Afrika, mpaka ku Scandinavian. Ndi kwina kotero, monga choncho. Gawo lalikulu la chaka, ine ndikukhulupirira, litengedwa ndi misonkhano ya kutsidya kwa nyanja. Kotero ndipempherereni ine, ine ndiyenera kupanga lingaliro lolondola.

30 Tsopano izo ziri ngati chiri chifuniro cha Ambuye; ngati sichoncho, ine ndiri wololera kupita kulikonse, malo aliwonse. Ziribe kanthu ndi kuti, ine ndikufuna kupita. Koma pamene ine ndiri wokhoza kukhala mu fumbi ili la dziko lapansi pomwe Mulungu anandiyikapo ine, ine ndikufuna ndizilalikira za chuma Chake chosawerengeka mpaka imfa itanditenga kuchokera mu thupi ili. Uko ndi kulimbika kwanga, mwa chisomo cha Mulungu, ngati Iye atangondithandiza ine. Ngati Iye achotsa dzanja Lake pa ine, mdierekezi adzandipha ine, kotero inu muzingopemphera kuti Mulungu asiye dzanja Lake la chifundo pa ine.

31 Ine sindikufunsa za chilungamo Chake; ine ndikufunsa za chifundo Chake. Mwaona? Tsopano, chilungano Chake, ayi, ine sindingathe kuyima nacho. Chifundo Chake chokha ndi chomwe ndikuchondelera, chifukwa ine ndikudziwa kuti sindiri woyenera, ndipo palibe amene ali. Ndipo ife kuli bwino kusafunsa chilungamo Chake. Ife tikufuna chifundo Chake.

32 Tsopano, usiku uno, pokhala ndiri wosasa pakhosi pang’ono, koma sindikanakana mwayiwu, kuti ndilankhule kwa gulu ili labwino la Akhristu. Dikirani, ndisanapange kulengeza uku, ndiroleni ine ndinene chinthu chimodzi. Pamene inu nonse muli mwa mtima umodzi tsopano, mu chiyanjano

chimodzi, ndipo zonse zikuyenda mokoma, ndiroleni ine ndingopereka kulankhula kochepa kwa maminiti awiri kwa mpingo wanga, onani.

³³ Tamverani, okonedwa anga mu Uthenga, anga... nyenyezi mu korona yanga, ngati ine ndidzakhale nayo imodzi, ogulidwa ndi Mwazi wa Yesu. Ine ndinachita ichi mwa cholinga, kubwerera chotere. Ife tinaganiza zimenezo pa ulendo wokasaka, M'bale Roy Roberson, M'bale Banks Wood, ndi ine, pa ulendo, kuti ife tikhoze kubweretsa, kubwerera. M'bale—M'bale Roy ndi ena tonsefe tinali kulankhula, ndipo za m'busa wathu, M'bale Neville, ndi mwamuna amene amakhala patsogolo panu nthawi zonse, kuchita ubusa ndi chirichonse, ife timamukonda iye; komabe, M'bale Neville pokhala m'busa wothandizira, zimawoneka zovuta pang'ono chabe kuti M'bale Neville kuti akankhidwire mkati mwa izo, onani. Kotero ife tinapemphera, ndipo zimawoneka ngati chinali chifuniro cha Ambuye kuti nditero. Tsopano, ine ndinafunsa Ambuye ngati Iye angathandize, ine ndikanachita mwakuyesetsa kwanga.

³⁴ Ndipo nditatha kupanga kudzipereka kwanga komwe, ndipo nditatha kupanga, kuchititsa mpingo kuti utero, tsopano, ngati Mulungu atidalitsa ife momwe Iye wakhala akuchitira mmisonkhano ingapo yapitayo, ndi kudzipereka kwa pang'ono kuja, Iye adzachita chiyani ngati ife titi tizingopitiriza ichi, mwaona? Ingopitirizani ichi. Tsopano mverani. Inu muli mu chikondi wina ndi mzake, momwe ine ndikukuwonerani inu mukuyima mtimipatamo, mmawa uno, ndi kumangolira, ndi manja anu okwezedwera kwa Mulungu, ndipo—ndipo Mzimu wokoma ukuyendayenda ponseponse pa inu.

³⁵ Tsopano inu musamamvera chinthu chimodzi choyipa chomwe mdierekezi ati anene. Mwaona? Ngati mdierekezi akuwonetsani inu zina, kapena kukuwuzani inu china choyipa, za mmodzi wa ziwalo za Thupi la Khristu, inu musamazikhulupirire izo. Pakuti, pamene inu muti muzikhulupirire izo, inu mumadetsa chokuchitikirani chanu.

³⁶ Ndipo ngati inu muwona mmodzi wa mamembala a Thupi la Khristu akuchita china choyipa, musamuwuze wina aliyense; koma pitani kwa membala ameneyo, ndipo ndi chikondi, ndi kukawona ngati inu simungawabwezere iwo kwa Khristu kachiwiri. Ndipo ngati inu simungatero, ndiye kawuzeni munthu mmodzi, kapena aloleni iwo apite nanu. Chitani izi momwe Malemba ananenera. Mwaona? Koma musa . . .

³⁷ Ngati wina ati, “Mulongo *Wakuti-ndi-wakuti*, kapena M'bale *Wakuti-ndi-wakuti*,” musakhulupirire liwu limodzi la izo. Inu ingozisiyani izo zipite. Chifukwa, kumbukirani, ndi mdierekezi akuyesa kukung'ambani inu mzidutswa. Tsopano ingoyang'anirani kuti iye alowamo, chifukwa iye adzatero. Tsopano inu lolani bambo wabwino wa nyumba, chikhulupiriro,

ayime pamenepo, ndipo inu musalandire chinthu chimodzi. Anthu awa akhazikitsidwa mu malo a M'mwambamwamba ndi inu, kuyanjana limodzi pozungulira madalitso a Mulungu, kumatengera m'gonero pa gome, ndipo Mzimu Woyera wachitira umboni kuti iwo ali ana a Mulungu. Kotero tiyeni tingokhala okoma zedi, a mtima wachifundo, okhululukira, okonda. Ndipo ngati munthu wina alankhula choyipa motsutsa inu, inu mulankhule zokoma motsutsa iwo. Penyani kukoma kumene kumabwera kwa inu pamenepo. Mwaona? Uko nkulondola. Nthawizonse musingobwezera zabwino kwa choyipa, chikondi kwa udani. Ndipo chabe. . .

³⁸ Kodi inu mukumva bwinoko, wokoma wapamtima, ka msungwana kakang'ono kumbuyoko? Izo nzabwino. Ine ndiri wothokoza kwambiri. Eya, anangobwerera cham'mbuyo. . . Iye anadzipiringiza mmbuyo mwa mfundo, ndipo Ambuye Yesu amubwezanso iye tsopano namupereka iye kwa msonkhano. Ife tiri othokoza chifukwa cha izo. Ndi zomwe ine ndinachokera ku guwa, mphindi zingapo zapitazo. Anati iwo anali "atapemphera ndi kupemphera, samakhoza kufika kwa Ambuye."

³⁹ Tsopano, tsimikizani kuti muchite zimenezo. Dzilumbirireni nokha izo, kwa Mulungu, "Mulungu, mwa chisomo Chanu, izo ndi zomwe ine nditi ndichite." Ziribe kanthu pamene wina anena zoyipa; bwezerani chabwino. Musaganize choyipa. Ngati inu muganiza choyipa, ndipo inu mukungolankhula izo mwa chinyengo, ndiye—ndiye—ndiye ndinu wolakwa. Inu musingopitirira kudzipereka nokha kwa Mulungu mpaka inu mumve bwino mwa inu za munthu ameneyo. Umo ndi momwe mungazichitire. Ndiye kukoma kwa madalitso a Mulungu kudzango, o, kudzangophimba moyo wanu. Umo ndi momwe mungakhalire mwachigonjetso, ndiye palibe chomwe chingakupwetekeni inu malinga ngati muli mu chikondi. Chabwino, inu mukuti. . .

⁴⁰ Onani, "Ngati inu muli ndi malirime, iwo adzatha. Ndipo ngati inu muli ndi chidziwitso, icho chidzasowa. Mauneneri, iwo adzalephera. Koma pamene muli ndi chikondi, chidzapirira kwa nthawizonse." Mwaona?

⁴¹ Ndipo musamangokonda iwo amene amakukondani inu okha, koma kondani iwo amene samakukondani inu. Pakuti, ndi zophweka kuti ine ndikonde aliynse amene amandikonda ine, koma yesani kukonda wina yemwe samakukondani inu. Apo ndi pomwe mungadziyese ngati inu muli Mkhristu kapena ayi; wina amene sakukondani inu, komabe, mu mtima wanu, inu mumawakonda iwo. Tsopano, ngati inu simuchita izo, ndiye zingogwiritsitsanibe kwa Mulungu. Ndi pamenepo, chifukwa ine ndikudziwa kuti ichi ndi Choonadi. Amen. Ine ndikudziwa kuti ndi Choonadi.

⁴² Tsopano ife titsegula Mawu opambana, tsopano, ku Bukhu la Ahebri, ndipo mutu wa 11, kwa Uthenga waufupi chabe. Pokhala wosasa mawu pang’ono, koma ine ndinali ndi madzulo abwino ndi abale ndi alongo. Ndipo sindinalalowe mpakana pafupi 6 koloko, ndipo ine ndinangothamangira m’chipinda ndipo ndinagwada pansu pambali pa bedi, ku chipinda chogonako, ndipo ndinapemphera kwa mphindi zingapo. Ndinadzuka, ndi kutenga Baibulo langa ndipo ndinayamba kuwerenga. Ndipo ine ndinawona magazini itayikidwa apo, ndipo ine ndinawatenga iwo, ndipo iwo anali atalembedwa mu chi Afrikaans, kotero ine sindikanaziwerenga zimenezo.

⁴³ Ndipo nthawizina, powerenga iwe, umadzakhudza liwu, ndipo liwu limenelo limakhala lamoyo kwa iwe. Umo ndi momwe mlaliki amapezera wake, uthenga wake. Kungoyamba kuwerenga, kuwerenga Baibulo, chinachake. Chinthu choyamba mukudziwa, iwe umakhudza chinachake, ndiye chinachake chimawonjezera ku chinacho, chinachake chimawonjezekera ku chinacho. Ndiye, umangolembe mzere pansu pake, ndi kungopita ku guwa ndi kukachiwerenga icho. Mulungu adzachita zotsalira zakezo. Onani, Iye adzasamalira zinazo.

⁴⁴ Tsopano, nthawizina umangotengeka kukafika kutali, mpaka umapanga tiziganizo pang’ono ta zimene, zolembe zapang’ono za malingaliro amene iwe unawaganiza. Nthawizina mu msonkhano, komwe iwe umangodza mofulumira ku nsanja, apo, kungowerenga pa timalingaliro tating’onoto tomwe unali nato, Mzimu Woyera umangodzafulumizitsa ito kwa iwenso. Ndachita izo nthawi zambiri.

⁴⁵ Tsopano Ahebri 11, tiyeni tiwerenge ndime yoyamba, kuyambira, ndipo tiwerenga ndime zingapo ndithu.

“Tsopano chikhulupiriro ndicho thunthu lake la zinthu zoyembekezeredwa, umboni wa zinthu zosapenyeka.

Pakuti mwa icho akulu anadzitengera mbiri yabwino.

Mwa chikhulupiriro ife tikumvetsa kuti mayiko anapangidwa ndi mawu a Mulungu, kotero kuti zinthu zimene zimapenyeka sizinapangidwe kuchokera ku zinthu zimene zikuwoneka.”

⁴⁶ Sizolemerera zimenezo? [Osonkhana ati, “Amen”—Mkonzi]. Ndiroleni ine ndiwerenge ndime yachitatu kachiwiri. Mverani mwatcheru.

“Mwa chikhulupiriro ife tikumvetsa kuti mayiko anapangidwa ndi mawu a Mulungu, kotero kuti zinthu zimene zikupenyeka sizinapangidwe kuchokera ku zinthu zimene zikuwoneka. (Mawu a Mulungu!)

Mwa chikhulupiriro Abele anapereka kwa Mulungu nsembe yoposa ija ya Kaini, imene anachitiridwa nayo

umboni kuti iye anali wolungama, Mulungu kuchitira umboni wa mphatso zake: ndipo ndi iyo . . . angakhale anafa komabe analankhula.

Mwa chikhulupiro Enoke anakwatulidwa kuti asawone imfa ndipo sanapezeke, chifukwa Mulungu . . . anamukwatula iye: pakuti asanakwatulidwe iye anali ndi umboni kuti iye anakondweretsa Mulungu. Zaka mazana asanu za moyonso!

Koma popanda chikhulupiro nkosatheka kumukondweretsa iye: pakuti iye amene adza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti iye ali, ndi kuti iye ndi wopereka mphotho kwa iwo amene amufuna iye modzipereka.

Mwa chikhulupiro Nowa, pochenjezedwa ndi Mulungu za zinthu zosapenyekabe, pochita mantha, anakonza chombo cha kupulumutsiramo a mnyumba yake; ndi . . . icho iye anatsutsa dziko, ndipo anakhala wolowa mnyumba wa . . . chilungamo chomwe chiri mwa—chomwe chiri mwa chikhulupiro.”

⁴⁷ Tsopano tiyeni ife tipemphere mwa kamphindi chabe, ndi kuweramitsa mitu yathu.

⁴⁸ Ambuye, Mulungu wathu Wachisomo Chopambana ndi Atate, ife tikudza tsopano mu Kukhalapo Kwanu kachiwiri, ndi kupereka mayamiko. Ndipo osati tsopano tikungomverera kuti ife tiri mu Kukhalapo Kwanu chifukwa chakuti taweramitsa mitu yathu kuti tipemphere, koma ife tikukhulupirira kuti ife tiri nthawizonse mu Kukhalapo Kwanu, chifukwa chakuti, “Maso a Ambuye amathamangira mtsogolo ndi mmbuyo kupyola mu dziko lapansi.” Ndipo Inu mukudziwa zinthu zonse, ndipo Inu mukudziwa maganizo a mtima.

⁴⁹ Chotero, Ambuye, chifukwa chomwe ife taweramitsira mitu yathu, ndi kuti tifunsire chofunika ichi, kuti Inu mukhoze kutikhululukira ife chifukwa cha zolakwitsa zathu zonse ndi zomwe takuchimwirani Inu, ndi kuti chifundo Chanu chitambasuliridwenso pa ife, mwakuti Inu mukhoza kutsegula milomo yathu kuti ilankhule ndi makutu athu kuti amve, ndi kuti Mawu Anu akhale enieni kwa ife, usiku uno; kuti ndime zohepa izi zimene ife tazisankha kuwerenga zikhoze kukhala thandizo lalikulu kwa chiwalo chirichonse cha thupi Lanu lachinsinsi pa dziko lapansi, Mpingo wanu wauzimu, Mpingo wa Woyambakubadwa, Mpingo uwo umene unagulidwa ndi Mwazi wa Yesu, umene watsukidwa ndipo wayeretsedwa, ndipo udzaperekedwa kwa Mulungu Tsiku ilo, wopanda banga kapena khwinya. Momwe ife tikukuthokozerani Inu, kuti tiri ndi chikhulupiro chokhulupirira kuti ndife ogawana nawo a ubwino uwu wa Mulungu, kupyolera mu chilungamo ndi chifundo cha Ambuye wathu Yesu!

⁵⁰ Tikupemphera tsopano kuti Inu muchize matenda onse. Kukuthokozani Inu chifukwa chomukhudza msungwana wamng'ono uja mphindi pang'ono zokha zapitazo, amene anapiringizika mu chipinda muja, ndi kupweteka; kumuona iye akuyenda, chikhulupiro changati cha mwana chiya, ndi kukulandirani Inu ndi chifundo Chanu. Ndipo ife tikukuthokozani Inu pa izi; ndipo tikupemphera kuti Inu mukumbukire Mlongo Baker wokonedwa wake wamng'ono uko mu Kentucky, ndi iwo amene M'bale Neville amawana, ndipo, O Mulungu, misasa yosawerengeka ya odwala kulikonse. Ndipo makamaka, Ambuye, iwo amene ali osapulumsidwa ndipo sakukudziwani Inu; ngati iwo amwalira mmachimo awo, iwo sangadze kumene Inu muli.

⁵¹ Ife tikupemphera kuti Inu mutipatse ife umboni ndi mphamvu, kulimba polankhula Mawu, ndi chidziwitso kuti tidziwe nthawi yolankhulira Iwo. Ndiyeno lankhulani kwa ife pamene ife tanena mokwanira, kuti ife tikhoze kuchokapo ndi kuwasiya anthu mu kudabwitsidwa, akuzizwa, za Mzimu Woyera wopambana ndi ntchito Yake. Tipatseni izi, Ambuye. Timvereni ife tsopano, ife tikupemphera, mu Dzina la Yesu ife tikupempha izi. Amen.

⁵² Ndipo ine ndikanakonda kulankhula kwa kanthawi kakafupi pa phunziro la mphamvu. Ife timaphunzitsidwa kuti munthu wachibadwa ali ndi mphamvu zisanu, ndipo mphamvu zisanuzo zimalamulira lake—lake... Kapena, Iye akupereka, Mulungu anamupatsa iye mphamvu zisanu izi, kuti azikhudzira kwawo kwapansi pano, ndipo mphamvu izo zimadziwika ngati: kupenya, kulawa, kukhudza, kununkhiza, kumva. Mphamvu zisanu izo zimene zimadziwika kwa munthu wachirengedwe, ndipo izo ndi zabwino, ndipo ife sitingachite kanthu kapena kukhala moyo wolunga pamene imodzi mwa mphamvu izi ilephera kuchitapo. Kupenya kwanu, kumva, kukhudza, kununkhiza, kapena kulawa, ife sitingakhale olunga popanda izo. Pali china chosowa, gawo lina la moyo lomwe sitingathe kulikhudza, popanda mphamvu imeneyo kuchitapo. Ndipo izo ndi zabwino ndipo izo ndi zogwiritsidwa ntchito, ndipo izo zinapatsidwa kwa ife ndi Mulungu.

⁵³ Mulungu anapereka mphamvu zimenezo, koma izo zinaperekedwa kwa inu ngati mphatso. Ndipo zimatengera momwe inu, komwe inu mumaziperekera mphamvu zimenezi, ndi komwe moyo wanu ukulamuliridwa, momwe inu mumaziperekera mphamvu zisanu zija. Inu muli... Chomwe inu mupenya, chomwe inu mumva, chomwe inu mulawa, kununkhiza, kapena kukhudza, chirichonse chomwe mphamvu izo zaperekedwako, izo zidzakulamulirani inu.

⁵⁴ Ndipo ife tiri othokoza kwa Mulungu kuti ife tiri ndi mphamvu zisanu, koma mopanda kutanthawuza kuti mphamvu zisanuzi zinaperekedwa kwa inu kuti zizikutsogolerani inu.

Izo zinaperekedwa kwa inu kuti muzilikhudzira dziko. Koma kunaperekedwa kwa inu mphamvu ya chisanu ndi chimodzi, ndipo, mphamvu ya chisanu ndi chimodziyo, ndiyo ya kwa Mkhristu yekha. Ndipo inu simungakhale ndi mphamvu ya chisanu ndi chimodzi iyi mpaka inu mutakhala Mkhristu; ili njira yokha yomwe inu mungakhozere kukhala ndi mphamvu yina yowonjezera kuposa zisanu za chirengedwe za munthu wa chirengedwe. Mphamvu ya chisanu ndi chimodzi imadziwika bwino, kwa Mkhristu, ngati chikhulupiriro. Ndi yomwe imalamulira ndi kukutsogolerani inu, ndipo ndi yapamwamba kwa mphamvu zina zonse. Ndi yapamwamba kwa mphamvu zonse, mphamvu zina zisanu zija.

⁵⁵ Tsopano, ine sindinganene kuti chifukwa chakuti ife timalandira mphamvu ya chisanu ndi chimodzi ndiye kuti mphamvu zisanu ndi zopanda ntchitonso. Inde, izo ziri. Mphamvu zisanu izo zinaperekedwa kwa inu ndi Mulungu, ndipo izo ndi zoti zizigwiritsidwa ntchito. Koma pamene mphamvu zisanu zichita mosiyana kwa Mawu a Mulungu, ndiye izo zikunama.

⁵⁶ Tsopano, mphamvu ya chisanu ndi chimodzi siyinganame. Ndiyo mphamvu yapamwamba. Ndipo ndi zomwe ine ndikufuna kulankhulapo. Mmawa uno ine ndinalankhula za: *Chizindikiro Chapamwamba*. Ndipo usiku uno za: *Mphamvu Yapamwamba*.

⁵⁷ Ndipo mphamvu yapamwamba ndiyo Mzimu Woyera, chikhulupiriro cha Mulungu chimene chimakhala mwa inu. Ndipo ngati inu mutalola mphamvu zisanu zikhale zodzipereka kwa mphamvu ya chisanu ndi chimodzi, iyo idzakutsogolerani inu ndi kubweretsa mphamvu zina zisanu zija pansi pa ulamuliro wa mphamvu yapamwambayo. Pakuti iyo ndi yapamwamba kwambiri pa mphamvu ya chirengedwe, monga munthu wauzimu ali wapamwamba pa wachirengedwe; ili patali monga kumwamba kuli, pamwamba pa munthu wachirengedwe ndi mphamvu zake zisanu. Imakupangitsa iwe kukhulupirira zinthu zimene iwe siwungaziwone. Imakupangitsa iwe kuchita pamene iwe siwukuganiza kuti mphamvu zisanu zija zikanaganiza za icho. Mdierekezi akhoza kulowa mwa mphamvu zisanu izi nanama kwa iwe, koma iye sangayikhudze mphamvu yapamwambayo. Iyo ili patali kwa kufikira kwake. Iyo imachokera kwa Mulungu. Iyo imatchedwa chikhulupiriro. Chikhulupiriro ndicho chinthu chopambanacho.

⁵⁸ Ndipo mphamvu zisanuzo sizimalamulira mphamvu ya chisanu ndi chimodzi, koma mphamvu ya chisanu ndi chimodzi imalamulira mphamvu zisanu. Mphamvu yapamwamba imalamulira mphamvu zachirengedwe. Ndipo—mphamvu zisanuzo ndizo kupenya, kulawa, kukhudza, kununkhidza, kumva. Ndipo mphamvu yapamwamba ndi chinachake chimene chidzakupangitseni inu kukhulupirira Mawu a Mulungu, pakuti ndicho chinthu chokha chomwe iyo idzalankhule za icho.

Ndipo Iyo idzakupangitsani kukhulupirira zinthu zimene inu simungaziwone, kuzilawa, kuzikhudza, kununkhiza, kapena kuzimva, chifukwa zimatengera Mawu a Mulungu. Ndipo idzapereka Mawu'wo kwa inu, ndi kukupangitsani inu kuyenda mosiyana kwa chinthu china chirichonse chomwe chiripo kupatula Mawu a Mulungu. Mwa chikhulupiriro, chikhulupiriro chimachita izo.

⁵⁹ Tsopano, popereka chitsanzo ichi, cha mphamvu, munthu wa chirengedwe amabadwa ndi mphamvu izi, kotero izo ndi mphamvu zoperekedwa mwachibadwa. Ndipo icho ndi chinthu chokha chomwe ati adzadziwe za icho, mwa kuganiza kwake mwaluntha. Iye akhoza kungolingalira ngati munthu, iye akhoza kupenya ngati munthu, iye akhoza kumvetsa ngati munthu, iye akhoza kumva ngati munthu; koma pamene iye akhala wolamuliridwa, kapena kusinthidwa, kapena ife tikhoza kuchitcha icho, “kubadwa kachiwiri,” ndiye ya chisanu ndi chimodziyo, mphamvu yapamwamba imamugwira iye. Ndipo, potero, mphamvu yapamwambayo imamukwezera iye mmwamba kufika pa malo amene iye ali ndi chikhulupiriro chokhulupirira zinthu zimene iye sangazimve, zinthu zomwe iye sakanakhoza kuziwona, kumvetsa komwe iye sangakumvetse. Iye amakhulupirira izo basi chifukwa iye akulamuliridwa mwa mphamvu ya chisanu ndi chimodziyo, mphamvu yapamwambayo. O, momwe ziri zonyumwitsa kuyidziwa iyo, ndi kuganiza momwe ziriri zophweka kuti uyikhulupirire iyo!

⁶⁰ Tsopano, inu simungazikhulupirire izo mpakana inu mutasinthidwanso. Baibulo linanena kuti, “Palibe munthu amene angamutche Yesu ali Khristu, kokha mwa Mzimu Woyera.” Ife tapyola mu zimenezo sabata yathayi. Ndipo chakhala chopunthwitsa chotero, kwenikweni kwa anthu okhulupirira mwa Chipentekoste, pamene iwo andimva ine ndikunena kuti. Yesu anati, mu Yohane Woyera 5:24, “Iye amene amva Mawu Anga nakhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali ndi Moyo Wamuyaya.” Moyo Wamuyaya umachokera kwa Mulungu, yekha. “Ndipo palibe munthu anganene Yesu ali Khristu, pokha mwa Mzimu Woyera.”

⁶¹ Inu mukungotenga chomwe winawake ananena, chomwe inu munaphunzira mwa luntha, chomwe inu munaphunzira mwa mphamvu zisanu za chirengedwe. Koma pamene mphamvu ya chisanu ndi chimodzi idzamo, Mzimu Woyera, Iwo umachotsa kulingalira konse mphamvu zisanu ndi imodzizi...mphamvu zisanu, nukukwezerani inu mmwamba kulowa mu mphamvu ya chisanu ndi chimodziyo, kukupangitsani inu kukhulupirira zinthu zimene simungaziwone, kuzilawa, kuzikhudza, kununkhiza, kapena kumva. Iyo imachita chinachake kwa inu. Ndiye inu mukhoza kunena kuti Yesu ali Khristu, chifukwa inu mwachitira umboni icho; osati chimene kuphunzira kwaluntha kwakuphunzitsani inu, koma chomwe chakuchitikirani.

62 “Mphamvu ya chisanu ndi chimodzi ndi yoti itani ndiye, M’bale Branham? Chifukwa chiyani mphamvu ya chisanu ndi chimodzi imadza?”

63 Mphamvu ya chisanu ndi chimodzi imadzera chifukwa ichi. Tsopano, mphamvu ya chisanu ndi chimodzi ndiyo chikhulupiriro, mphamvu yapamwamba. Tsopano ngati... Mphamvu ya chisanu ndi chimodzi imadzera chifukwa ichi chokha, ndicho, kupangitsa mphamvu zisanu zija mwa inu kukana chirichonse chomwe chiri chotsutsana ndi Mawu a Mulungu. Ndi zomwe mphamvu ya chisanu ndi chimodzi imachita. Lemba limalankhula za “kuchotsa kulingalira.”

64 Za—za, mwaona, mphamvu zisanu zidzatero, inu mukhoza kulingalira, “Chabwino, tsopano, chifukwa chiyani mwamuna yu, ndipo chifukwa chiyani. . .?”

65 Koma mphamvu ya chisanu ndi chimodzi siyimawona zimenezo konse. Ndi yapatali kwambiri kupyola izo! Ndi yapamwamba kwambiri kuposa izo, mpaka kuti iyo ilibe ngakhale zolingalira konse ndi iyo. “Ife tikuyikhulupirira iyo!” Iyo ili kutali kuposa chirichonse chimene mphamvu zisanu zija zikanati zinene za icho. Tsopano ife tikukonzekera msonkhano wa machiritso, onani. Ife tikuyikhulupirira iyo! Inu mumayenda mwa mphamvu ya chisanu ndi chimodziyo, inu mumalankhula mwa mphamvu ya chisanu ndi chimodziyo, inu mumakhala moyo mwa mphamvu ya chisanu ndi chimodziyo, inu mumafa mwa mphamvu yachisanu ndi chimodziyo, ndi kuwuka mwa mphamvu yachisanu ndi chimodziyo. Mphamvu yapamwambayo, chinachake chomwe chiri mwa inu, chomwe chiri chosiyana ndi zomwe munthu wachibadwa ali.

66 Munthu wachibadwa ali ndi izi zokha, ndipo izo zonse ziri bwino ngati izo zingabweretsedwe mu kumvera kwa mphamvu ya chisanu ndi chimodzi. Ngati malingaliro a chibadwa ati, awerenga Mawu a Mulungu nati, “Awo ndi Mawu a Mulungu,” iwo akunena Choonadi. Koma ngati iwo awerenga, nati, “Onsewo si Mawu a Mulungu. Kapena, kapena, Iwo anali. Ndi chinachake, Anali nthawi yina, koma Iwo sali tsopano.” Ndiye mphamvu yachisanu ndi chimodziyo imadzamo, niiti, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.” Onani, ndiko kusiyana kwake.

67 Ndicho chifukwa chake kuti anthu ambiri amalephera kuchiritsidwa. Iwo akuyesa kubwera ndi kumvetsa kwaluntha. Iwo amati, “O, ine—ine ndimachita *izi*, kapena ine ndimakhulupirira *izi*, ndi zina zotero.”

68 Koma ngati mphamvu yachisanu ndi chimodzi ija ikutero, ndiye palibe chinthu chimene chiti chidzawagwededeze iwo kuwachotsa ku mphamvu ya chisanu ndi chimodziyo. Mphamvu ya chisanu ndi chimodzi yadza pa anthu kudzawapangitsa iwo kukana chirichonse chosiyana kwa Mawu a Mulungu.

Mawonekedwe aliwonse, mawonekedwe aliwonse amene ali osiyana kwa lonjezo la Mulungu, mphamvu yachisanu ndi chimodzi imati icho palibe apo, ngati Mkhristu yemwe wabadwa kachiwiri.

⁶⁹ Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, wachikunja wina, wosakhulupirira, amazembera kwa Mkhristu nati, “Tsopano yang’anani pano, palibe chinthu monga Mzimu Woyera uwo. Inu mwangolakwitsa, mwa Icho. Inu mwapenga, ngati inu mukukhulupirira chinthu chotero monga Icho. Palibe chinthu chotero monga Icho.”

Mphamvu yachisanu ndi chimodziyo imangopita molunjika kukagwira ntchito.

⁷⁰ “Ndiroleni ine ndikusonyezeni inu, mu Baibulo, pomwe inu simungalandirire Mzimu Woyera. Ndipo, muwona, ine ndikhoza kukusonyezani inu pamene ophunzira anawulandirira Iwo, koma—koma . . .”

⁷¹ “Eya, chabwino,” inu mukuti, “Onani,” mphamvu yachisanu ndi chimodzi ikulozerani inu pamwamba niiti, “koma Iye anati, ‘Lonjezo liri kwa inu ndi kwa ana anu.’”

⁷² “Chabwino, izo zimatanthawuza ana awo. Izo, izo sizimatanthawuza kwa inu. Izo siza kwa inu.”

⁷³ Koma mphamvu yachisanu ndi chimodziyo imadziwa bwino. Bwanji? Iyo Ili kale mwa inu. Iwo anazinena izi mochedwa kwambiri. Inu mwayilandira Iyo kale.

⁷⁴ Anthu amene anaphunzitsa kuti, “Palibe chinthu chotero monga Mzimu Woyera,” sakudziwa za zomwe iwo akulankhula.

⁷⁵ Monga mnyamata uja, nthawi ina, akuyengula apulo, ndipo anafunsidwa ndi wachikunja, kutsutsana za msonkhano. Iye anati, “Kodi inu mukufuna chiyani, kodi inu mukufuna chiyani kuno?”

⁷⁶ Iye anati, “Ine ndikufuna ndikufunsemi inu funso.” Pamene iye anali kudya apulo akusangalala nayo, wophweka kwambiri, wonga motero, amawoneka ngati munthu wopusa, tsitsi liri wirawira pa nkhope yake, ndipo dzino limodzi linachoka patsogolo; ndipo wachikulire, atavala jekete ya ovalolo yakale ili bii. Iye anati, “Funso limodzi lokha ine ndikufuna ndikufunsemi inu.”

⁷⁷ Wachikunjayo nkuti atangoti, “Palibe chinthu chotero monga Mulungu. Zonse ndi zotengeka. Ndi zamkhutu kwa izo, ndizo zonse zomwe ziri.”

⁷⁸ Ndipo mnyamatayo anati, “Ine ndikufuna kukufunsemi inu funso, bambo. Kodi apulo iyi ikukoma kapena ikuwawasa?”

Iye anati, “Chabwino, nanga ine ndidziwa bwanji? Ine sindikudya iyo.”

Iye anati, “Izo ndi zomwe ine ndimaganza basi,” nayenda chobwerera mmbuyo.

⁷⁹ Nanga inu mudziwa bwanji, pamene inu simunawalawepo Ambuye? Mukudziwa bwanji, pamene inu simunalandirepo Mzimu Woyera, kaya Iye ali weniweni kapena Iye siali? Inu mukudziwa bwanji ngati chiri chikhulupiriro ndi mphamvu? Inu mudziwa bwanji kuti kulibe “chimwemwe chosakambika ndi chodzaza ulemerero,” pamene inu simunalawe kuti muchiwone icho? Mphamvu ya chisanu ndi chimodzi imakutsogolerani inu kwa Icho. Mphamvu ya chisanu ndi chimodzi imafotokoza Icho kwa inu.

⁸⁰ Palibe mphamvu zaluntha konse, zidzabweretse konse Icho kwa inu. Mphamvu zaluntha zidzalingalira niziti, “Bwanji, ndi kuwerenga maganizo. Ndi chinachake mwa njira *iyi*, ndipo ndi kutengeka ali nako anthuwa.”

⁸¹ Koma pamene mphamvu yachisanu ndi chimodzi ilowamo, iyo imakana zinthu zina zonsezo, nimusuntha munthu molunjika kulowa mu zifuwa za Mulungu. “Iye amene adza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti Iye ali, ndi wopereka mphotho kwa iwo amene amufuna Iye modzipereka.” Mwa chikhulupiriro! Mwa chikhulupiriro, Abrahamu! Mwa chikhulupiriro, Isaki! Mwa chikhulupiriro, Yakobo! Onse mwa chikhulupiriro! Ndi mphamvu yachisanu ndi chimodzi yomwe imachita izo. Mphamvu yachisanu ndi chimodzi imakana zisonyezo zonse, zisonyezo zonse, chirichonse chosiyana ndi Mawu a Mulungu, kumverera kulikonse, kutengeka.

⁸² Wina ati, “O, chabwino, ine ndinapemphereredwa; koma ine sindikumva bwino konse.”

⁸³ Mphamvu yachisanu ndi chimodzi siikanayimitsidwa njo kwa izo. Mphamvu yachisanu ndi chimodzi ingati, “Ilo ndi bodza! Ine ndikumva bwino. Ine ndikupeza bwino. Mulungu anatero, izo zimakhazikitsa icho. Amen! Mulungu anatero.” Mphamvu yachisanu ndi chimodzi imadyera pa Mawu a Mulungu okha.

⁸⁴ Mphamvu yapamwambayo, ndi yapamwamba, pamwamba pa zimphamvu. Ndi mphamvu yopambana. Ndi chikhulupiriro. Ndi nyonga yomwe imakondoweza niyiyendetsa. Amen. Ndi chinachake chomwe chimakupangitsa iwe kuchita zinthu zimene siwunaganizepo kuti ukanachita. Ndi mphamvu yachisanu ndi chimodzi, mphamvu yapamwamba.

⁸⁵ Inu mumapemphereredwa. Tinene kuti munali—muli ndi dzanja lopunduka ndipo munapemphereredwa, dzanja lanu, inu munabwera pamwambapo ndipo inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu. M’busa akupemphererani inu, inu nimubwerera. Munthu wakale wachibadwayo adzanena izi, “Iwe siukumva mosiyana m’dzanja lakolo. Iwe siuli bwino koposa momwe unaliri kale.” Koma mphamvu yachisanu

ndi chimodziyo imadza, niiti, “Limenelo ndi bodza! Iwe wapemphereredwa, izo zatha basi.” Amen.

⁸⁶ Monga mkazi uja anabwera ku msonkhano wathu nthawi imodzi, ndipo iye anadza ku msonkhano, awiri a iwo. Iwo anadutsa pa nsanja. Iwo anali atawona kudziwa kwa za mumtima. Akazi amenewo anango—anangomezedwa kwathunthu. Iwo onse anali Akhristu enieni. M’modzi anadza, ndipo Mzimu unadza nuti, “Inu mukuvutika ndi vuto la mmimba.”

Ndipo nkhope yake inawala. Iye anati, “Izo nzoona.”

⁸⁷ Ndipo Mzimu Woyera unati kupyolera mwa ine, unati, “Ndipo ndi nsungu. Zimayamba chifukwa cha khalidwe la manjenje. Inu mwayesedwa ndi dotolo wina, ndipo iye anati kuthi inu simunga . . . kapena ziyenera ku—kapena nkofunika kuti akuchiteni opreshoni, kuti azichekepo.”

Iye anati, “Liwu lililonse la izo ndi lowona!”

⁸⁸ Ndiyeno powona kuti anali wokhulupirira kwambiri chotero, ndiye Iwo unati, “Dzina lako ndi Abiti *Wakuti-ndi-wakuti*, iwe ukuchokera *Kwakuti-ndi-kwakuti*, ndi malo akuti-ndi-akuti.”

Iye anati, “Izo nzoona!”

⁸⁹ Chinali chiyani icho? Mphamvu ya chisanu ndi chimodzi kuchigwira icho. Mphamvu ya chisanu ndi chimodzi ndi Mzimu Woyera zinali kuyima mbali kwa mbali. Mzimu Woyera unali kulankhula, mphamvu ya chisanu ndi chimodzi imati “Amen.” Ndi zimenezo. Chinachake chinayenera kuchitika.

⁹⁰ Pamene Marita anathamangira kukamupeza Yesu, ndipo pamene iye anati, “Ambuye!” Penyani mphamvu yachisanu ndi chimodzi. “Ngati Inu mukanakhala pano, mchimwene wanga sakanafa; koma ngakhale tsopano, chirichonse chomwe Inu mudzapempha Mulungu, Mulungu apereka icho kwa Inu.” Ndi imeneyo mphamvu yachisanu ndi chimodzi.

⁹¹ Yesu anadzikokera Yekha palimodzi, nati, “Ine ndine Chiukitsiro ndi Moyo; iye amene akhulupirira mwa Ine, ngakhale iye anali atafa, komabe iye adzakhala moyo; aliyense amene akhala moyo nakhulupirira mwa Ine sadzafa konse. Kodi iwe ukukhulupirira izi?”

⁹² Kodi iwe unena chiyani, kulingalira? Patakhala munthu atagona apo, wakufa, mphusi zikukwawa kupyola mwa iye.

⁹³ Koma Iye anangotsiriza kunena kuti Iye anali Chiwukitsiro ndi Moyo. Amenewo ndi Mawu a Mulungu. Mphamvu yachisanu ndi chimodziyo, kupyola chisamaliro cha adotolo, kupyola malingaliro a kufufuza kwa sayansi. Kunoza zonse, kunyoza kulingalira konse, ndi kuzitaya izo pansi. Bwanji? Iyo ikuchitira umboni kwa Mawu a Mulungu, “INE NDINE. Ine sindine ‘Ine ndidzakhala, Ine ndinali.’ INE NDINE TSOPANO! Ndine

Chiwukitsiro ndi Moyo,” Munthu. “Iye amene akhulupirira mwa Ine, ngakhale iye anali atafa, komabe iye adzakhala moyo; ndipo aliyense amene akhala moyo nakhulupirira mwa Ine sadzafa konse. Kodi iwe ukukhulupirira izi?”

⁹⁴ Iye anati, “Eya, Ambuye,” mphamvu yachisanu ndi chimodzi, “Ine ndikukhulupirira kuti Inu ndinu Mwana wa Mulungu, amene anayenera kudza mu dziko.”

“Mchimwene wako adzaukanso.” O, mai!

⁹⁵ Kumanda iwo anapita! Iwo awiri, limodzi, chinachake chinayenera kuchitika. Imeneyo inali mphamvu ya pamwamba, ndi Mulungu atayima pamenepo, chinachake chinayenera kuchitika. Mphamvuyo inali mphamvu yapamwamba, inali Mulungu. Panali chinachake chimamuwuzwa Marita zimenezo. Iye anali atamuwona Iye. Anamudziwa Iye. Anamuzindikira Iye kuti ndi Mesiya amene. Ndipo iye anadziwa, ngati atangokafika kwa Iye, ngati akanangokafika pafupi ndi Iye nakafotokoza vutolo, kungomva lonjezo limodzi kuchokera kwa Iye, ndi zonse zomwe iye ankafuna. Pamene Iye anati, “Ine ndine Chiwukitsiro ndi Moyo; iye amene akhulupirira mwa Ine, ngakhale iye atamwalira,” ndi zokhazo zomwe Marita ankafuna kumva, zonse zomwe iye anafuna. Chifukwa, mphamvu yachisanu ndi chimodzi, mphamvu yapamwamba, chikhulupiriro chake, chinali kumusuntha iye kuti amuvomereze Iye, kumukhulupirira Iye.

⁹⁶ Mkazi uyu, pamene anachoka pa nsanja, anali PAKUTI ATERO AMBUYE, “Pita kunyumba nukadye. Yesu Khristu wakukhalitsa iwe bwino.” Iye anapita kunyumba.

⁹⁷ Usiku umenewo, mzake wa iye wokhala pafupi naye, anali wachitatu kapena wachinayi kumbuyo kwake, ndipo iye anali ndi chotupa chachikulu pakhosi pake. Ndipo apa iye anadza, wotengeka ndi iye—mnansi wake, anali woti achiritsidwe nsungu zimene zimamusawutsa iye kwambiri. Ili linali limodzi mwa mavuto zana, zikwi za iwo. Ndipo chotupa ichi chachikulu chitaturukira pa khosi pake, ndipo iye anabwera. Ine ndinatani, “Panalibe amene akanachita kufufuza icho. Koma inu muli okondwa ndi chinachake, inu mwasangalatsidwa, chifukwa mkazi uja amene wakhala apoyo ndi wapafupi nanu.”

⁹⁸ Mzimu Woyera! Iye anaganiza, “Angadziwe bwanji izi mu dziko mwamuna ameneyo? Chiyenera kukhala Chinachake kuti chiwulule izi kwa iye.”

⁹⁹ Kotero pamene icho chinanenedwa, Iwo unati, “Inu mukuganiza za khosi lanu.”

“Inde.”

“Kodi mukukhulupirira icho chichoka?”

“Ine ndikukhulupirira izi,” iye anati, “ndi mtima wanga wonse.”

100 Ine ndinati, “PAKUTI ATERO AMBUYE, pita kunyumba ndipo ukalandira machiritso ako.”

101 Munthu wachibadwa anayang’ana pozungulira ndipo sanawone chizindikiro chirichonse. Mkazi amene anali ndi nsungu anapita kunyumba nakayesa kudya, ndipo, mai, iye akanafa. O, munthu wachibadwa, mphamvu yachibadwa, ya kumverera inafotokozerabe kuti nsunguzo ziripo.

102 Kotero patapita pafupifupi sabata kapena awiri, iye anadzera kwa apafupi naye, kwa anthu ake onse, ndipo mpingo, kuchitira umboni, “Ambuye andichiza ine.”

Ndipo iwo anati, “Kodi inu mukumadya tsopano?”

103 “Ayi, osati kwenikweni zonse zimene ine ndikuzifuna. Koma,” iye anati, “Ndine wochiritsidwa kale, pakuti ndi mikwingwirima Yake ine ndachiritsidwa.” Ziribe kanthu chomwe chinali, iye anachiritsidwa basi.

104 Ndipo mmawa umodzi, ana anali atapita ku sukulu, ndipo iye anamva njala kwenikweni. Iye anali atayima, akutsuka mbale, cha pa zenera. Iye anadza ku msonkhano, msonkhano wina patapita pafupi chaka. Ndipo iye anali akutsuka mbale, ndipo pamene iye, chinthu choyamba, anamverera kukhudza kwenikweni kwachirendo kukuyenderera. Ndipo iye anaganiza, “Chimenecho chinali chiyani? Amangowona ngati akufuna kufuula.”

105 Ndipo mwamuna wake anamuwuzwa iye, anati, “Wokonedwa, iwe usiye kunena za machiritso aja,” nati, “chifukwa,” ngakhale iye anali Mkristu, nati, “iwe ukubweretsa chitonzo pa Cholingacho.”

106 Ungabweretse chitonzo bwanji pamene ukuchitira umboni kwa Mawu Ake? Ukhoza kubweretsa chitonzo ngati siuchitira umboni wa Icho.

Nati, “Ngati iwe unachiritsidwa, unachiritsidwa.”

107 Iye anati, “Mwamuna uja anayima nandiyang’ana ine mmaso, nandiwuzwa ine momwe ndiriri ndi zinthu zomwe ine ndinachita, ndi kuti ndine yani, ndi komwe ine ndinachokera,” Iye anati, “Ine ndinali mu nyumbayo maminiti khumi ndi asanu, pamene iye anadza pa nsanja. Mdzikoli mwamuna uyu angadziwe bwanji zimenezo? Ine ndinali ndisanamuwone iye mmoyo wanga, ndipo iye anandiwuzwa ine, “PAKUTI ATERO AMBUYE, iwe wachiritsidwa.” Ndipo iye anati, “Ine ndikhulupirira zimenezo mpaka nditafa.” Iye anati, “Ine ndidzakhulupirira izo basi.” Kotero iye ndi mchemwali wake wamng’ono, mzake, anachita pangano kwa Mulungu, kuti agwiritsitsa chikhulupiro chimenecho.

108 Mmawa umenewo, iye anangomva mwachirendo kwenikweni, ndipo mwa maminiti pang’ono iye anamva njala. Kotero ana anali atasiya phala lina m’mbale, mbale yaying’ono;

ndipo anati phala nthawizonse limangomuwocha iye. Ngati aliyense anakhalapo ndi nsungu, inu mukudziwa chomwe chiri. Kotero iye anafikira natenga nadyako kangapo phalalo. Ndipo, “O, mai,” iye anati, “Ine ndiyenera kulipira chifukwa cha icho, ine ndikuganiza, koma limodzi la masiku awa ine ndidzakhala bwino.” Koma iye anazindikira kuti iye anali ndi njalabe, kotero iye anangotsiriza mbaleyo. Iye anayembekezera maminiti pang’ono, kuona chomwe chinachitika. Panalibe chomwe chinachitika; amangomva bwino, wanjalabe. Iye anakazinga mazira ake angapo, nadzithirira kapu ya khofi, natengapo tositi, ndipo iye anakhaladi ndi phwando lake lenileni. Iye ankangodya zonse zomwe akanadya. Iye anapitirira kutsuka mbale, ndipo pafupi theka la ora, iye anakhalanso ndi njala. Popanda zopweteka zina.

¹⁰⁹ Iye anavala kachisoti kake kakang’ono, ndipo mu msewu iye anapita, kunyumba ya woyandikana nayeyu. Ndipo pamene iye anafika kumeneko, iye anamva, iye ankaganiza kuti mwina kwachitika imfa m’banjalo. Iwo anali kupokosera, nafuula, namayenda ponseponse. Mayiyo anali atagona mochedwa mmawa umenewu, ndipo anadzuka, kuyang’anira pa chotupa chomwe chinali pakhosi lake, ndipo chinali chitachoka mu usikuwo. Chinali chiyani chimenecho? Mulungu pantchito.

¹¹⁰ Kuno ku Cadle Tabernacle, pamene ife tinali ndi msonkhano uja, mnyamata wopunduka uja amene anadza mmenemo ndipo iye anapemphereredwa. Ambiri a inu munali kumeneko kuti mukamuwone iye. Iwo anamubweretsanso iye mu chipinda changozicho. Billy ananditsogolera ine kwa iye. Iwo anamubweretsa iye pa nsanja kwa usiku utatu kapena unayi, apo pa . . . mu chipinda. Iye sanapeze khadi la pemphero, kotero iwo anamuyika iye mu chipinda changozi. Ine ndinalowa mmenemo ndi kumupempherera iye, kuyang’ana pa iye. Iye anati, “Bambo Branham, kodi inu mungandiwuze ine chitonhozo china?”

Ine anati, “Inde, bwana, mwana. Poliyo wakufikitsa iwe motere.”

Iye anati, “Uko nkulondola.”

¹¹¹ Ine ndinati, “Dzina lako ndi *lakuti-lakuti*. Iwe wachokera ku malo ena ake.”

“Uko nkulondola,” iye anatero. Iye anati, “Bwanji za machiritso anga?”

Ine ndinati, “Ndi mikwingwirima Yake iwe unachiritidwa.”

¹¹² Iye anapita kwawo, akuchitira umboni, akumupatsa Mulungu mayamiko. Ndipo iye anabweretsa chitonzo chotero, iwo ankatero, apafupi, mpaka Lamlungu limodzi gulu la atumiki linalowa nilikhala pansu pomwe iye anali ndipo anati, “Iwe uyenera kusiya kuchita izo. Iwe ukubweretsa chitonzo pa Cholingachi.”

113 Ndipo mnyamata wamng'ono atakhala kumeneko, anati, “Bambo, ngati inu mukadamakhala pamene ine ndiri, ngati inu mukadakhala mu mpando umene ine ndakhalamo, inu sibwenzi mutayesa kundibera ine chiyembekezo chotsiriza ine ndiri nacho, mwa Khristu.” Anati, “Ndi mikwingwirima Yake ine ndachiritsidwa.” Ndipo iye sananene zoposa izo. . . Atakhala pamenepo, wopuwala, mapazi, manja, thupi, nsana. Ndipo asananene zoposa izo, ndipo kuchokera mu mpando iye anapita, akulemekeza Mulungu.

114 Chiyani? Mphamvu zake zachibadwa zinati iye azikhala pamenepo; adokotala anati azikhala pamenepo nthawizonse, kapena malingana ngati ali moyo. Koma mphamvu ya chisanu ndi chimodzi ikuti, “Ndi mikwingwirima Yake ine ndachiritsidwa.” Ndipo iye sakanakhala ndi chochita chirichonse. . . Ndi kutayira kunja chirichonse chosiyana ndi chimene Mulungu ananena. Ndicho chimene mphamvu ya chisanu ndi chimodzi yaperekedwera.

115 John Rhyn wokalamba, osati R-y-a-n, R-h-y-n. Kunali wopemphetsa wakhungu mu Fort Wayne, ndipo uko ndi kumene tinapita tsiku lija ndipo iye anapemphereredwa mu msonkhano. Uwo unali usiku limba lisanayimbe “*Msing'anga Wamkulu tsopano alipafupi*,” popanda wina pafupi nayo. Ndipo pamene iye anali wakhungu, iye anali Wachikatolika, mwa chikhulupiriro. Ndipo iye—iye anachoka mu mzere, ndipo ine ndinayang'ana pa iye, ndipo ine ndinati, “Dzina lanu ndinu *wakuti-ndi-wakuti*, John Rhyn.”

“Inde.”

“Ndinu wopemphetsa pa kona. Inu mwakhala wakhungu kwa zaka.”

“Inde, uko nkulondola.”

“Ndinu Wachikatolika, mwa chikhulupiriro.”

“Uko nkulondola.”

116 Ine ndinati, “PAKUTI ATERO AMBUYE, inu mulandire machiritso anu.”

Anati, “Ndikuthokoza inu, bwana.”

Ine ndinati, “Thokoza Ambuye.”

Iye anati, “Koma ine sindikutha kupenya.”

Ine ndinati, “Izo ziribe chochita ndi ichi. Inu mwachiritsidwa.”

117 Ndipo iye anati, iye anapitirira, iwo anamuthandizira iye kutsika pa nsanja. Munthu wachibadwayo samakhoza kupenya kanthu. Iwo samakhoza kupenya zotsatira kuchokera pa izo konse. “Bwanji,” anati, “iye ali wakhungu monga iye analiri kale.”

118 Kotero awiri a amzake anamubweretsanso iye namuyika iye mu mzere wa pemphero kachiwiri, namuyendetsanso iye. Howard anamulola iye kudutsa. Pamene iye anabwereranso, iye anati, “Bambo, inu munandiuza ine kuti ndinachiritsidwa.”

Ine ndinati, “Inu munandiwuza ine kuti inu munandikhulupirira ine.”

119 Iye anati, “Ine ndikukukhulupirirani inu. Ine ndiribe zifukwa zosakukhulupirirani inu.” Anati, “Inu mwandiwuza ine zinthu zonse mu moyo wanga,” ndipo iye anati, “Ine sindikudziwa choti ndingachite.” Nati, “Kunali mkazi kumbuyo uko amachitiraa umboni kuti iye anali ndi khosi lotupa maminiti ochepa apitawo, ndipo icho chachoka.”

120 Ine ndinati, “Ndiye ngati inu mukundikhulupirira ine, bwanji inu mukundifunsa ine? Ine ndikukuwuzani inu Mawu a Mulungu.”

121 Iye anati, “Ndichite chiyani ine, bwana?” Podziwa kuti iye anali Wachikatolika ndipo amayenera kukhala ndi china chogwirika chomwe iye akhoza kugwirako, ine ndinati, “Dzingochitirabe umboni, ‘Ndi mikwingwirima Yake ine ndachiritsidwa,’ ndipo uzimupatsa Iye mayamiko.”

122 Munthu wachikulireyo, kwa masabata awiri otsatira, kapena atatu, iye anayima pa kona ndipo iye amagulitsa mapepala, iye amakhoza kufuula, “Yapadera! Yapadera! Ambuye alemekezeke, ine ndachiritsidwa! Yapadera! Yapadera! Ambuye alemekezeke, ine ndachiritsidwa!”

123 Pamene iye anabwerera ku msonkhano usiku wotsatirawo, ine sindinathe konse kulalikirira, chifukwa cha iye. Iye amadzuka nafuula, “Aliyense akhale chete! Ambuye alemekezeke chifukwa chondichiritsa ine! Ambuye alemekezeke chifukwa chondichiza ine!” Ngati Wachikatolika, iye sanadziwe momwe angachigwirire chikhulupiriro, koma iye anadziwa ngati iye apitirira kunena pa icho, napitirirabe, kupitirirabe, kupitirirabe, mpaka mphamvu ya chisanu ndi chimodziyo ingapite kukagwira ntchito. Uko nkulondola. “Ambuye alemekezeke chifukwa chondichiza ine!”

124 Iye anali atayima pa kona, akufuula, “Ambuye alemekezeke chifukwa chondichiza ine! Yapadera! Ambuye alemekezeke chifukwa chondichiza ine!”

125 Iye amakhoza kuyenda mu msewu, ndipo kumeneko wina anabwera pafupi, nati, “Uli bwanji, John?”

126 “Ambuye alemekezeke chifukwa chondichiza ine! Ndiri bwino.” Ndipo iwo anamuseka iye, namunyoza iye.

127 Ndipo mnyamata wina wamng’ono wamanyuzi anamutsogolera iye kometetsera, kuti akamumete, pafupi masabata awiri kapena atatu otsatira kuchokera pa msonkhano. Ndipo wometayo anamuyika iye pa mpando, nathira zometera

pa nkhope yake. Ndipo iye anati, “John,” iye anati, “ine ndamva . . .” Wofuna kuchenjera pang’ono, ndipo iye anati, “Ine ndamva kuti iwe unapita kukamuwona wa machiritso Auzimu pamene” [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. “apa.”

Iye anati, “Inde, ine ndinapitako.”

¹²⁸ Iye anati, “Ine ndamva kuti iwe unachiritsidwa,” kungofuna kumuserewula iye.

¹²⁹ Ndipo bambo wachikulireyo anati, “Inde, Ambuye alemekezeke, Iye anandichiza ine,” ndipo maso ake anatseguka. Kuchokera mu mpando wometerapowo iye anapita, ndi nsalu pa khosi pake; wometa kuyesa kumugwira iye, ndi lezara mu dzanja lake. Ndipo kumka mu msewu iwo anapita! Bwanji? Mawu a Mulungu anali atapita kukagwira ntchito.

¹³⁰ Georgie Carter wamng’ono atagona kutsidyako, amene inu nonse mukumudziwa, anthu ena ali muno pafupi, atagona mmenemo kwa zaka zisanu ndi zinayi ndi miyezi isanu ndi itatu, osatha konse . . . popanda koma kuyala nsalu pansu pa iye, zochokera mu impyso ndi matumbo. Iye ankalempera mapaundi okwanira makumi atatu ndi asanu. Atagona kutsidya mu Milltown, Indiana. Ndipo makolo ake anali a mpingo umene . . . Pamene ine ndinapita kukachititsa msonkhano kumeneko ku mpingo wa Baptisti mu Milltown, ndi kupempherera odwala, mpingo umenewo unati, “Ngati membala aliyense wa gulu ili akamuwona wotenthekayo, ife tiwachotsa iwo.” Ndipo abambo ake anali adikoni.

¹³¹ Koma iye anali atatenga bukhu langa laling’ono, lotchedwa, *Yesu Ali Yemweyo Dzulo, Lero, Ndi Nthawizonse*. M’bale Hall ananditengera ine kwa iye, madzulo ena. Amayi ake anathawa mnyumbamo, analibe chochita ndi izo. Ine ndinalowamo ndi kumupempherera iye. Anati, “Chabwino, nanga bwanji msungwana uja wa a Nale?” Iye anadziwa za masomphenya.

¹³² Ine ndinati, “Awo anali masomphenya, mlongo. Ine ndikhoza kungopemphera. Inu muli ndi chikhulupiriro.” Kanthu kakang’ono kosawuka kanali kataphunzitsidwa motsutsa izo.

¹³³ Masiku pang’ono kuchokera apo, ine ndinali kuyimirira uko ndikubatiza. Iye anali kumeneko, akulira; chimene iye anali atalonjeza kuti adzabwera nadzabatizidwanso, mu Dzina la Yesu Khristu, ngati Mulungu atangomuchiza iye.

¹³⁴ Ndipo uko, iye, miyendo yake yaying’ono pafupi kukula kwa mtengo wa tsache. Iwo samakhoza ngakhale kumuyika iye pa machira ake. Amayi ake, komabe mkazi wamng’onoyo, anakhala pamenepo, atasweka ndi khunyu, ndi mutu wa imvi, kumupenya mwana wake wamkazi atagona pamenepo akufa mwa mainchesi. Matenda a mziwalo za akazi, ndipo anayenderera mkati mwake monse. Iye amalempera mapaundi ena makumi asanu mphambu zisanu ndi ziwiri, ine ndikuganiza anali, iwo anamuyeza iye. Samakhoza kumudzutsa iye mmwamba mokwanira kuti ayike

chiwaya pansi pake; amachita kusolola mkwamba kuchokera pansi pake, wa mpirapira. Zaka zisanu ndi zinayi ndi miyezi isanu ndi itatu, iye anali akugona pamenepo, osatha konse kudzutsa mutu wake kuti ayang'ane mtengo umene unali cha pazenera.

¹³⁵ Tsiku lina, nditayima mmbuyo, pamwamba pake pa phiri, kwa a George Wright, Mzimu Woyera unati kwa ine, “Dzuka pa mapazi ako.” Ndipo ine ndinayang'ana, ndipo uko kunali Kuwala kukuwala kudutsa mu mtengo wa nkhalangoyagaru, anati dzera cha ku njira ya kwa a Wright, kapena, “Dutsira njira ya kwa a Carter.”

¹³⁶ Pamene ine ndinafika kumeneko, Ambuye Yesu anali atamuwonetsa amayi ake chizindikiro chakuti ine ndikubwera. Ndinadzafika kwa msungwana uyo atagona apo pa bedi ilo, wolefuka kwambiri mwakuti iye samakhoza ngakhale kukweza kapu yamalovu. Amayi ake amayigwirizira iyo, ku “ha,” kuyesa kulavulira mu kapu ya malovu, ndi TB. Ine ndinati, “Mulongo Georgie. Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, anakomana nane kutsidya mu nkhalango, pafupi theka la ora lapitalo, ndipo anandiua ine kuti ndibwere kudzayika manja pa iwe. PAKUTI ATERO AMBUYE, ima pamapazi ako!”

¹³⁷ Mphamvu ya chisanu ndi chimodzi inapita kukagwira ntchito, Mphamvu inamukhudza msungwana uyo, kwa nthawi yoyamba mu zaka zitatu...kapena zaka zisanu ndi zinayi ndi—ndi miyezi isanu ndi itatu, iye anali asanayime ndi mapazi ake, analumpha nayima ndi mapazi ake, nathamangira kuseri kwa nyumba, ndipo akudalitsa mitengo ndi udzu ndi chirichonse, ndipo analowa nakakhala pansi pa limba nayamba kuyimba, “*Pali Kasupe wodzaza ndi Mwazi, wowukha kuchokera mmitsempha ya Emanuele.*”

Bwanji? Kulingalira kukanakhoza kuponyera pansi . . .

¹³⁸ Iye sakanakhoza kuchita icho. Ine sindikudziwa tsopano. Ine sindidzaziwanso. Mphamvu ya Mulungu yokha ndi yomwe inamugwira iye nimuyimika. Miyendo yake siinali yayikulu *chotere* kuzungulira, mmwamba umu polumikizirana; panalibe chonga iyo, ngati mitengo ya tsache. Izo zinali zaka khumi ndi ziwiri zapitazo, kapena khumi ndi zinayi, ndipo lero iye ndi wamphamvu ndi wathanzi, akuyendera Ambuye Yesu.

¹³⁹ Chinali chiyani icho? Nthawi yoyamba, panalibe kanthu kamawoneka ngati kakuchitika, koma kulingalira kukanakhoza kunena kuti izo sizingachitike. Koma, m'bale, iye anagwiritsitsa kwa Mawu amenewo. Ngati Mulungu anakhoza kumutenga msungwana uja wopuwala ku Salemu, msungwana uja wa a Nale, anakhala wolumala ndi kupuwala, ndipo manja ake amazendewera pansi *chotero*, anakhoza kumuchiza iye, Iye akhoza kumuchizanso iye. Iye anakhulupirira izo.

¹⁴⁰ Ndipo M'bale Hall, atagona kutsidya, akufa ndi khansara; munthu yemweyo ananditengera ine kumeneko. Dotolo wake mu Milltown anamutumiza iye kwa dotolo uyu mu New Albany, kumusi kuno, ndiko uko ku Chipatala cha Edward Woyera. Ine ndinayiwala. . . Iye anabweretsa ana anga; munthu wabwino, dotolo wabwino. Iye anamuyesa iye, nati, "Khansara." Nati kwa Dokotala Brown, kumusi mu Milltown, nati, "Iye akufa." Dokotala Brown anati, "ine ndimaganiza choncho."

¹⁴¹ Anamutengera iye kwa mlongo wake kumusi kuno, amene ali—wachibale wa Bambo Kopp, anakhalapo woweruza mu mzinda. Ndipo pamene iwo anafika kumusi uko, anati, "Ingomusungani iye kuno mpaka atafa."

¹⁴² Ndipo iwo ananditumira ine kuti nditsikireko. Ine ndinapita, tsiku ndi tsiku, ndi mkazi wanga, kumbuyo uko. Iye timamupempherera M'bale Hall. Ine ndimamukonda iye. Iye anali mmodzi wa owatembenezira anga kwa Khristu. Ndipo iye amatsikiratsikira, ndipo iye samakhoza kusuntha manja ake.

Akazi a Hall anati, "Billy, palibe china chomwe iwe ungachite?"

¹⁴³ Ine ndinati, "Palibe chirichonse ine ndikuchidziwa, Mlongo Hall. Ine sindikumva liwu kuchokera kwa Ambuye. Iye tika. . ." Ine ndinati, "Ine ndikufuna dotolo wanga ayang'ane pa iwo."

Anati, "Dotolo wanu ndi yani?"

Ine ndinati, "Dotolo Sam Adair."

¹⁴⁴ Ndipo ine ndinamuyitana Sam. Sam anati, "Chinthu chokha, ine ndingamutumize iye ku Louisville, Billy, kukamujambula ndi zinthu." Anati, "Ine ndikupatsa iwe zotsatira." Iwo anatumiza ambulasi uko, anamunyamula iye, namutenga iye; nabwerera.

¹⁴⁵ Sam anandiyitana ine, ndipo anati, "Billy, iye ali ndi khansara wa mchiwindi. Iye sitingadule kuchotsa chiwindi chake, ndipo iye nakhala moyo." Anati, "Iye ndi mlaliki, iye ayenera kukhala bwino tsopano. Inu mukhoza kungomuwuza iye kuti akupita."

¹⁴⁶ Ine ndinati, "Iye ali wokonzeka kupita, Sam. Koma, chinthu chake ndi chakuti, ine ndikungodana ndi kumuwona iye akupita. Iye ndi m'bale wanga, ndipo ine ndimamukonda iye."

Ndipo ine ndinaganiza, "O Mulungu, ndichitireni ine chinachake."

¹⁴⁷ Ine ndinayamba kupita kukasaka agologolo mmawa umenewo. Ine ndinayang'ana kunja kusanache, palibe yemwe anali kunja mu bwalo; ndinanyamula mfuti ndikuwuyamba kudutsa mnyumba. Apo panali apulo yakale yowoneka-moyipa itapachikidwa pa khoma. Ine ndinaganiza, "Chifukwa chiyani Meda anaiika iyo pa khoma?" Ine ndinayang'ana, ndipo ina ndi ina ndi ina, mpaka asanu ndi mmodzi a iwo anapachikidwa apo. Ine ndinachotsa chipewa changa ndipo ndinagwada pa maondo

anga, pansi. Ndinayang'ana pamwambapo, ndipo kenako apulo wamkulu wokongola kwambiri anatsika nadya maapulo onsewo. Ine ndinayang'ana atayima pamwambapo, ndipo apo panali Kuwala komweko (komwe kuli pa chithunzi *icho* uko) akuyima apo, kukuzungulirazungulira, anati, "Ima pa mapazi ako. Pita ukamuwuze Bambo Hall, 'PAKUTI ATERO AMBUYE,' iye siafa, koma akhala moyo."

¹⁴⁸ Ine ndinapitako ndikukamuwuzwa iye. Iye sanali wosiyana konse, koma iye anakhulupirira izo. Iye anagwiritsa kwa icho. Panalibe kusintha kulikonse, kunawoneka ngati. Tsiku linadutsa, popanda kusintha. Tsiku lachiwiri, popanda kusintha. Pafupi tsiku lachitatu, iko kunayamba. Ndipo pano iye ali moyo lero, zitatha zaka ndi zaka.

¹⁴⁹ Ine ndinazindikira atakhala pompano, Akazi a Weaver. Ayi, ine sindikulakwitsa. Pamene mwana wawo wamkazi anabwera, pambuyo pa machiritso a Margie Morgan, ine ndinapita kumeneko ndipo uko kunalibe kanthu kamene mkazi akadachita. Iye akadakhocha kufa mumaora ochepa otsatira. Iwo anamulasa, kapena pawiri, iwo akanakhocha kumupatsa iye, ndipo zinali zokhazo. Iye anali ndi opareshoni yachikazi, khansara anali atayenderera mu nsana wake. Iwo anayimwaza iyo pamene iwo anamung'amba, ndipo apo panalibe chochita kwa mkazi. Ine ndinkafuna kulankhula naye iye za machiritso.

¹⁵⁰ Koma iye anati, "Bwana, ndinu mtumiki wa Ambuye Mulungu, ndipo ine sindiri woyenera kuti inu mubwere mu nyumba mwanga." Kudziwerengera yekha wosayenera kuti mtumiki bwere. Iye anati, "Ine ndakhala moyo. Ine ndavina. Ine ndachita zinthu zimene ine sindimayenera kuchita. Ine ndagwiritsapo chilankhulo choyipa, kapena china chirichonsecho." Iye anandiwuzwa ine machimo ake, ndipo iye anati, "Ine sindiri woyenera wa icho."

¹⁵¹ Ine ndinawona iye akugunda mzere woyenera. Iye akanayenera kutero kuti amulowetse Khristu mkati *umu* mphamvu yapamwambayo yachisanu ndi chimodzi isanapite konse kukagwira ntchito.

¹⁵² Ife tinagwada pansi. Ine ndinalankhula kwa iye za "ngakhale machimo ako akhale ngati kapezi." Iye anapereka moyo wake kwa Ambuye Yesu Khristu. Ndipo pamene iye anatero, iye anati, "O, o, ine ndikumva mosiyana kwambiri. Chinachake chachitika kwa ine. Chinachake chachitika kwa ine. Ine ndikufuna kugwirana chanza ndi yense wa inu."

¹⁵³ Ndipo nthawi yomweyo ine ndinayang'ana panja ndipo ine ndinamuwona iye mu masomphenya, akubwerera kuseri kwa nyumba ku khola la nkuku. Ine ndinati, "Akazi a Weaver, PAKUTI ATERO AMBUYE MULUNGU, mupanga ulendo wopita ku khola la nkukulo, ndipo mukhala moyo."

154 Iye sakanapita momwe amamverera; khansara anali atamudya iye. Iye sakanapita mwa zomwe adotolo ananena; iye amafa. Ndipo izo zakhala, ine ndikuganiza, zaka khumi ndi zinai, khumi ndi zisanu zapitazo, Akazi a Weaver? [Akazi a Weaver ati, “Khumi ndi zinai.”—Mkonzi]. Zaka khumi ndi zinai zapitazo. Iye anazandima mpaka kuno ku Kachisi pamene iye anali kudwala, sizimawoneka ngati anali wokhoza kudzuka pa kama, mikono yaying’ono yopuwala yakale; chifukwa iye anamulonjeza Mulungu kuti adzabwera nadzabatizidwa mu Dzina la Yesu. Iye tinamunyamula iye kuchoka mu chikuku, pafupi, umo mu chikuku, kumutengera iye mu dziwe ndi kumubatiza iye mu Dzina la Yesu. Ndipo ndi uyo wakhala apoyo, usiku uno. Yang’anani pa iye ngati inu mukufuna kuwona umboni wa umoyo. Bwanji? Kuponyera pansi malingaliro ndi kufufuza kwa sayansi, ndi china chirichonse, chifukwa mphamvu yachisanu ndi chimodzi inapita kukagwira ntchito. Ndizo izo.

155 Yang’anani, ndiroleni ine ndingonena ichinso, kwa miniti chabe. Yesu anadutsa pafupi ndi mtengo nthawi yina, ndipo iwo unali mtengo wa mkuyu. Ndipo Iye anayang’ana pa mtengo wa mkuyu. Tsopano, chonde, musaphonye ichi. Iye anayang’ana pa mtengo wa mkuyu, ndipo umo munalibe nkhuu pa iwo. Ndipo Iye anati, Iye anawutemberera mtengowo nati, “Palibe munthu ati adye kuchokera mwa iwe.”

156 Ophunzira anayang’ana pozungulira; mtengowo unawoneka monga umawonekera nthawizonse. Ora limodzi zatachitika izo, iwo unawonekabe chimodzimidzi. Mulungu sanatsegule dziko ndi kuwumeza iwo. Mulungu sanatumize mphezi yogawanika kuchokera mu mlengalenga ndi kuwuwotcha iwo kuti ukhale makala. Iye akanakhoza kuchita izo, zedi Iye akanakhoza. Iye sanachite zinthu zimenezo.

157 Chinachitika ndi chiyani? Mtengowo unali utatembereredwa. Chikhulupiriro cha Mulungu chinali chitayikidwa motsutsa moyo wa mtengowo. Panalibe china chogwirika mukadakhocha kuchiwona. Koma pansi pa nthaka, pansi mu mizu ya mtengo, imfa inali ikulowerera. Iwo unali utatembereredwa. Mphamvu yachisanu ndi chimodzi inali itabwera motsutsa iwo. Iwo umayenera kufa. Iwo unayamba kufa kuchokera ku mizu.

158 Ndi chinthu chomwecho chikuchitika ndi khansara, ndi chinthu chomwecho chimachitika ndi chotupa, ndi chinthu chomwecho chimachitika ndi nthenda iliyonse pamene mphamvu yachisanu ndi chimodzi ya Ambuye Mulungu iwuka pamwamba motsutsa icho. Anati, “Satana tuluka mmenemo.” Inu mwina simungawone chikhalidwe chathupi nthawi yomweyo, koma chikhulupiriro icho chimagwira uko momwemo basi. Iwo watembereredwa. Mphamvu ya chisanu ndi chimodziyo siyingathe, mphamvu yapamwambayo siyingalole

iwo kupitirira. Iyo siyingasamale momwe inu mukumverera, momwe mukuwonera, momwe mukuchitira. Iyo singakhale ndi chinthu chimodzi kuchita ndi icho. Mawu a Mulungu anali atayikidwa. Mphamvu yachisanu ndi chimodzi yawugwira iwo. Ndi zokhazo. Icho chinapita kukagwira ntchito; khansara akuyamba kufota. Iye akufa kuchokera ku mizu, ndipo watha. Ndithudi.

¹⁵⁹ Mwa mphamvu yomweyi yokankha kwambiri ya chisanu ndi chimodzi, maufumu agwa, asanjikizana khoma limodzi pa lina.

¹⁶⁰ Mwa mphamvu iyi yachisanu ndi chimodzi, Nyanja Yofiira inakankhidwa mmbuyo, ndipo nthaka youma inakonza njira kwa ana a Mulungu kuti athawirepo.

¹⁶¹ Mwa mphamvu yomweyi ya chisanu ndi chimodzi, Samusoni ananyoza Afilisiti chikwi okhala ndi zida ndi nthungo. Iye analibe njira yodzitetzera yekha, koma fupa la chibwano cha bulu wa kuthengo. Ndipo mphamvu ya chisanu ndi chimodziyo inapita kukagwira ntchito, ndipo iye anakantha nacho Afilisiti chikwi. Aleluya!

¹⁶² Mwa mphamvu iyi ya chisanu ndi chimodzi, akufa awukitsidwa. Mwa mphamvu iyi yachisanu ndi chimodzi, zozizwitsa zazikulu zachitidwa.

¹⁶³ Ndiyo kukankha kwamphamvu kwambiri komwe kunakanthapo dziko, ndiyo mphamvu ya pamwambayo, yotchedwa mphamvu ya chisanu ndi chimodzi. Iyo ilibe chochita ndi *iyi* pansi pano; ngati iyi pansi pano inena za iyo ndikuti “amen” kwa Iyo, nzabwino, inu mukuyendabe; koma popanda kusamala zomwe iyi ikuchita, khulupirirani *Iyo*. Uko ndi kumene mphamvu, “ngati inu mukhulupirira mu mtima mwanu.” Mphamvu yanu yachisanu ndi chimodzi, ya kuganiza, imakhala mu ubongo wanu, koma mphamvu yanu ya chisanu ndi chimodzi imakhala mu mtima mwanu. Inu mumakhulupirira ndi mtima wanu. Kuvomereza kumachitika ndi pakamwa. Inu *mumakhulupirira* ndi mtima wanu, inde, bwana, mphamvu iyo ya chisanu ndi chimodzi, kukankha uko kwamphamvu.

¹⁶⁴ Mverani, chifukwa cha mphamvu ya chisanu ndi chimodziyo, analipo mneneri yemwe anaponyedwa mu khola la mikango. Ndipo chifukwa cha mphamvu iyo ya chisanu ndi chimodzi, mikango siyinathe kumudya Daniele. Iyo siyikanakhoza. Iyo siyikadakhoza kufika pafupi naye, chifukwa cha mphamvu iyo ya chisanu ndi chimodzi, mphamvu yapamwambayo.

¹⁶⁵ Mwa mphamvu yomweyo ya chisanu ndi chimodzi, ana atatu Achihebri anaponyedwa mu ng’ango ya moto ndipo iwo ananyoza malawi a moto. Mphamvu ya chisanu ndi chimodziyo! Kulingalira konse kukanakhoza kutsimikizira kuti iwo awotchedwa nafa iwo asanalowe umo, koma mphamvu yachisanu ndi chimodzi iyo inawakhazikitsa iwo mmenemo kwa maora awiri kapena atatu. Ndipo pamene iwo anatsegula

ng'anjoyo, iwo anawona Mmodzi atayimirira pakati pawo, wonga Mwana wa Mulungu. Ndiyo mphamvu ya chisanu ndi chimodzi. Moto siwukadatha kutentha iyo. Inde, bwana.

¹⁶⁶ Inali mphamvu ya chisanu ndi chimodzi yomweyo, nthawi ina, yomwe Mtumwi Petro anali kugona mu ndende, ndipo iwo anali oti akamudule iye mutu, tsiku lotsatiralo. Ndipo kumusi ku nyumba ya Yohane Marko iwo anali ndi msonkhano wa pemphero. Mphamvu iyo ya chisanu ndi chimodzi inayamba kusunkhana pozungulira ndendeyo, kumene iye anali ataphimbika ndi pemphero. Mphamvu iyo yachisanu ndi chimodzi inapita kukagwira ntchito. Lawi la Moto linalowa pa zenera ndipo linamukhudza Petro, ndipo linati, "Tiyeko, tuluka muno." Mphamvu yachisanu ndi chimodzi!

¹⁶⁷ Inali mphamvu yachisanu ndi chimodziyo imene siyikanamusiya Paulo Woyera kuti amire pa nyanja ija yamphamvu, pamene kabwato kakang'onoko kanakhuta madzi. Inali mphamvu ya chisanu ndi chimodzi yomwe inamuteteza iye kuti asamire, mphamvu yapamwambayo. Inali mphamvu iyo yachisanu ndi chimodzi, imene, pamene njoka inamuluma iye pa dzanja, iye anayisasira iyo m'moto. Inali mphamvu ya chisanu ndi chimodzi imene inachita zimenezo.

¹⁶⁸ Inali mphamvu ija yachisanu ndi chimodzi imene inamuwukitsa Yesu Khristu kwa akufa, atatha Iye kugona mu nthaka, chifukwa Iye amakhulupirira Mawu a Mulungu. Anati, "Phwasulani thupi ili, ndipo Ine ndidzaliwukitsanso ilo pa tsiku lachitatu. Pakuti Davide anati, "Ine sindidzasiya Mmodzi Woyera Wanga kuwona chivundi, ine sindidzasiyanso moyo Wake mu Hade.""" Inali mphamvu yapamwambayo. Tayani pansi kulingalira kwa mphamvu *izi*. Khulupirirani mphamvu yapamwamba, mphamvu ya chikhulupiriro, yomwe Yesu Khristu akupereka.

¹⁶⁹ Mwa mphamvu yomweyo, Mulungu analankhula pamene kunalibe kanthu. Kodi mphamvuyo ndi chiyani? Mphamvu yapamwambayo ndi Mulungu, chikhulupiriro cha Mulungu mwa inu, gawo la Mulungu limene limabwera mwa inu ndi kukupatsani inu mphamvu yapamwamba. Mwa mphamvu yomweyo yapamwamba, Mulungu anakonza dziko palimodzi ndi zinthu zomwe panalibe ndipo sizimawoneka. Iye analankhula Mawu Ake ndipo anakhulupirira Mawu Ake, ndipo dziko linagwedezeka mkukhalapo. Ulemerero!

¹⁷⁰ Mphamvu yachisanu ndi chimodzi, mphamvu yapamwamba, O Mulungu, itsanulireni iyo pa ine. Iperekeni iyo kwa ine ndi kwa aliyense yemwe akuyisowa iyo. Tsanulirani mphamvu Yanu yachisanu ndi chimodzi mwa ine, Ambuye. Ine ndikulolera kupereka zisanuzi, nzeru zanga zomwe, malingaliro, kuponya pansi kulingalira konse, Ambuye. Lolani Mawu Anu akhale woona, ndipo mawu a munthu aliyense abodza. Kulingalira

kulikonse, kukayikira kulikonse, kuponyedwe kutali, ndipo mundilore ine ndiyende mwa mphamvu yapamwamba, mphamvu ya Mzimu Woyera.

¹⁷¹ Kodi inu simukuyifuna iyo? Ndicho chinthu chimene ife tikuchifuna. Mulungu akudalitseni inu, abwenzi. Ndicho chimene inu mukusowa. Mphamvu yapamwambayo ifunsa chinachake ndipo iyo ikudziwa kuti Iye apereka icho. Ndi yokakamizika, “Pakuti iye amene adza kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti Iye ali, ndi wopereka mphotho kwa iwo amene amufuna Iye mwakhama.

¹⁷² Ngati mphamvu yachisanu ndi chimodzi iti, “Mulungu amasunga Mawu Ake. Ine ndikudzipereka ndekha kwa Iye. Ine ndikupereka zonse ndiri nazo, kwa Iye. Mphamvu yanga ikuti ichi chipangitsa izi kuchitika, chikhulupiriro changa mu Mawu a Mulungu,” ndiye itchani chirichonse, chosiyana ndi icho, ngati kuti panalibe.

¹⁷³ Abrahamu anakomana ndi Mulungu, ndipo Mulungu anati, “Iwe ukhala ndi mwana mwa Sara.” Iye makumi asanu ndi awiri mphambu zisanu, ndipo mkaziyo makumi asanu ndi limodzi mphambu zisanu. Abrahamu anatcha chirichonse chimene sichinali, chinali chosiyana kwa icho, ngati kuti panalibe. Iye anayenda ngati kuti iye anamuwona Mulungu, ndipo iye—iye anakhulupirira.

¹⁷⁴ Iye anatcha chirichonse chimene chimanena kuti iye sanali, kulingalira kulikonse, china chirichonse chimene... Adotolo mwina ananenapo, “Bwanji, Abrahamu, iwe ndi wamkulu kwambiri kuchita izo.” Izo sizikupanga kusiyana kulikonse zimene adotolo ananena, zimene wina aliyense ananena, zomwe malingaliro ake omwe ananena, zomwe china chirichonse chinanena. Mulungu anali wolondola, ndipo iye anakhala ndi icho.

¹⁷⁵ Ndiyo mphamvu yachisanu ndi chimodzi, mphamvu yapamwamba. “Mulungu, iperekeni iyo kwa ine. Mulungu, ndiroleni ine ndikhale ndi zambiri za iyo,” kuti ndikatumikire kwa anthu Ake, ndilo pemphero langa.

¹⁷⁶ Mmawa uno, pamene mayi awo anabweretsa mwana wamng’ono wa mutu wofiirayo, atayima pano, misonzi ikuyenderera chotsikira mmasaya awo. Ine ndinati, “Chavuta nchiyani, mlongo?”

¹⁷⁷ Iye anati, “M’bale Branham, ali ndi vuto la mitsempha.” Ine ndinamverera chinachake chikuwuka. O, Iye ali thandizo lopezekeratu mu nthawi za mavuto.

¹⁷⁸ Kuno osati kale kwambiri, Billy ndi ine timayenda mu msewu, tikuwongolera. Anyamata ena achikuda anadza mu msewuwo ndipo iwo anali kuyendetsa mwaliwiro kwambiri, ndipo iwo anayigunda galimoto ya mmbali ndipo inagudubuzika niyigudubuzika kugudubuzika, ndipo inawatayira anyamata

mu msewu monse, ndipo mnyamata mmodzi anakanirira pansi pa galimotoyo ndi nsana wake utagonera pa galimotoyo. Anyamatawo analumphira kunja nayamba kuyidzutsa iyo. Iye anati, “O, chonde musatero, nsana wanga ukuthyoka! Musatero! Mundipha ine! Mundipha ine! Musachite izo!”

179 Ndipo iwo anati, “O, ife tiyenera kuyichotsa iyo kwa iwe, iyo ikuyaka moto.” Anati, “Isiyeni . . .”

180 “Musayisunthe iyo, mukundifinyira ine ku imfa! Musachite izo! Musachite izo!”

Ine ndinafuula pansipo, “Mwana, kodi ndiwe Mkristu?”

Iye anati, “Ayi, bwana.”

Ine ndinati, “Iwe kuli bwino upemphere.”

Iye anati, “Inde, bwana.”

181 Mphamvu yachisanu ndi chimodzi inapita kukagwira ntchito. Nnayenda chozungulira mpaka kuseri kwa galimotoyo, ndipo ine sindidzadziwa mpaka pa Chiweruzo, koma, zonse mwadzidzidzi, galimoto iyo inatembenuka ndipo iyo inali itamusiya iye, ndipo iye analumpha mmwamba ndipo anali bwino. Chinali chiyani icho? “Thandizo lopezekeratu mu nthawi za mavuto!”

182 Ife tinali kubwera kuchokera ku...Dona wamng’ono wachikuda anali kuyendetsa galimoto mu msewu, Plymouth yatsopano, pafupi mailosi mazana anayi pa iyo. Iye anali kuyendetsa pa liwiro labwino kwambiri. Ndipo ine ndinayiwona galimotoyo. Inakawombetsa karankashafiti yake yonse mpaka mu mtengo. Billy ndi ine tinayima. Kunali chisanu, msewu woterera patsogolo pathu, koma panthawiyo kunali kowuma. Msungwana . . .Mphepo inali kuwomba molimba, uko mu Minnesota, mpaka inawulutsa galimotoyo. Iwe ukukumbukira izo, Billy? Ine ndinathamangira kumeneko kwa iye. Ndipo kumeneko, iye atakhala pamenepo, iye anati, “O, ine ndikufa. Ine ndikufa.” Iwo anayitana ambulasi.

183 Ambulasi inabwera, ndipo iwo anali ndi munthu wakufa atagona kumbuyo kwa ambulasi. Anati, “Ine sindingamutenge iye.”

184 Ndipo chotero mchikumbe anati, “Chabwino, tumiza winawake, msanga, mkaziyo akufa.”

Ine ndinayendera kumeneko, ndipo ine ndinati, “Dona, miniti chabe.”

185 Iye anati, “O, musandikhudze ine, bwana. Musandikhudze ine. Nsana wanga!”

186 Ine ndinati, “Dona, kodi ndinu Mkristu?” Iye anayang’ana pa ine. Ndipo ine ndinati, “Ndine mtumiki wa Uthenga. Ngati inu mukufa, nanga ziri bwanji inu ndi Mulungu?”

Iye anati, “Bwana, ine ndikufuna kukhala, pakali pano.”

¹⁸⁷ Ndipo mphamvu yachisanu ndi chimodzi inapita kukagwira ntchito. Mphamvu ya Mulungu inatsika pansi. Iye anakhoza kuyenda kuchoka mgalimoto, popanda aliyense womuthandizira iye. Mphamvu ya Mulungu, kukhalapo, “Thandizo lopezekeratu mu nthawi za mavuto.”

¹⁸⁸ Ife timayenda mwa chikhulupiriro. Ife timakhala moyo mwa chikhulupiriro. “Olungama adzakhala moyo mwa chikhulupiriro.” Ife tiyenera kumakhala moyo chotero. Ndi angati akufuna kukhala ndi zambiri za yachisanu ndi chimodzi, mphamvu yapamwamba? [Osonkhana, “Amen.”—Mkonzi].

Ndiye tiyeni tiweramitse mitu yathu, pamene ife tikupemphera.

¹⁸⁹ Ambuye opambana, Mulungu wathu ndi Atate wathu, Inu muli abwino kwambiri kwa ife. Inu munatipatsa ife mphamvu zisanu kuti tizikhala nazo moyo ndi kumayenda nazo, mu dziko ili, kapena ku—kapena kulikhudzira dziko. Ife tikhoza kukhudza zinthu zomwe—zomwe ziyenera kukhudzidwa, ndi manja athu, zinthu zogwirika. Inu munatipatsa ife kumva, kuti tizikhoza kumva. Ife tiri okondwa kwambiri chifukwa cha izo, kuti ife tikhoza kumamva Mawu a Mulungu, ndipo, mwa izo, “chikhulupiriro chimadza pakumva, kumva Mawu a Mulungu.” Ife tiri othokoza chifukwa cha zokhudzira zisanu ndi chimodzi izi, Ambuye. Titasunga zonsezo mmasiku onse a moyo wathu.

¹⁹⁰ Koma mulole mphamvu yapamwambayi, mulole mphamvu ya chikhulupiriro, yomwe ndi ya kwa wokhulupirira, chifukwa iye ayenera kukhala nayo iyo kuti akhulupirire. Ambuye, tipatseni ife zambiri za iyo. O, itsukeni iyo, Ambuye, ndipo tiyeseni ife, ndipo tidzazeni ife nawo ubwino Wanu ndi mphamvu Yanu. Tiloleni ife tiyende masiku onse a moyo wathu, ndi mphamvu yachisanu ndi chimodzi, ndi mphamvu ya chikhulupiriro, ndicho choperekedwa ndi Yesu Khristu yekha. Kuti chimene ife tichipempherera, ife tikhulupirire kuti ife tichilandira icho, osakhala ndi kukayika mu mtima wathu, ndipo Inu munalonjeza kuti izo zidzachitika.

¹⁹¹ Iwo amene anakweza manja awo mmwamba, Ambuye, ine ndikuwapempherera iwo. Iwo anali ndi zosowa. Inu mukudziwa chimene izo zinali. Ine ndikupemphera kuti Inu muzikwaniritse izo, aliyense wa iwo. Mulole izo zikwaniritsike, zokhumba zawo. Ine ndikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

Chikhulupiriro mwa Atate, chikhulupiriro
mwa Mwana,
Chikhulupiriro mwa Mzimu Woyera, atatuwa
ali Mmodzi;
Ziwanda zidzanjenjemera, ndipo ochimwa
adzawuka;
Chikhulupiriro mwa Yehova chinjenjemeretsa
chirichonse

¹⁹² Kodi inu munayamba mwayimvapo imeneyo kale? Tsopano popanda zoyimba, miniti chabe.

Chikhulupiro mwa Atate, chikhulupiro
mwa Mwana,
Chikhulupiro mwa Mzimu Woyera, atatu awa
ali Mmodzi;
Ziwanda zidzanjenjemera, ndipo ochimwa
adzawuka;
Chikhulupiro mwa Yehova chinjenjemeretsa
chirichonse.

¹⁹³ Uko nkulondola. O, mai! Chikhulupiro chopambana! Chopambana, chikhulupiro chaulemerero. Mulungu, ndipatseni ine chikhulupiro. “Mwa chikhulupiro, Abrahamu. Mwa chikhulupiro, Isaki. Mwa chikhulupiro Abele anapereka kwa Mulungu nsembe yopambana koposa ya Kaini; iye pokhala chiferebe, komabe anachitira umboni.” O, momwe tikusowera chikhulupiro! Ine ndimamukonda Iye. Ine ndikufuna chikhulupiro chambiri. Chokhumba changa mu moyo uno, ndiponso kwa chaka chatsopano chikudzachi, ndicho chikhulupiro chambiri mwa Mulungu. Mulungu, chotsani kukayikira kulikonse kumene kuli mmalingaliro anga, ngati pangawuke kumodzi. Satana amamenya pa ine, iye amamenya pa inu, iye amayesa kuponya mivu yake. Koma ndikhale nacho chishango cha chikhulupirocho nthawizonse patsogolo panga, kuti chitsutse machenjerero a mdierekezi, kuteteza, kugwetsera kumbali mivi yake ya moto, ndilo pemphero langa lodzipereka. Mulungu akudalitseni inu.

¹⁹⁴ Muli ndi chirichonse cholankhula, M’bale Neville? [M’bale Neville ati, “Ayi, chabe. . .”—Mkonzi]. Bwerani. [M’bale Neville akulengeza, umboni, ndi pemphero lotsirizira].



MPHAMVU YAPAMWAMBA CHA59-1227E
(A Super Sense)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingelezi pa Lamlungu mmawa, Disembala 27, 1959, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1993 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1993 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org